


# ZITSEKO MU CHITSEKO

 . . . kuno mmawa uno. Ine ndimaganza za nthawi yanga yobwera ku Flagstaff—nthawi yoyamba. Izo zakhala pafupifupi, ine ndikuganza, pafupifupi zaka sarte-eyiti zapitazo, mwinamwake forte. Ine ndinali kuyankhula za kukwera phiri. Kunalibeko chipale, koma Model-T yanga yaying’ono sinkatha kukwera phirilo. Iyo inkayenda mailosi sarte pa ora, koma izo ndi fikitini mbali *iyi* ndi fikitini mbali *iyi*, inu mukudziwa, pa ina mwa misewu iyi imene ife tinali nayo kuno. Ndipo iyo inali ndithudi . . .

<sup>2</sup> [M’bale pa nsanja akuti, “Bwanji inu simukutiiza ife ndakatulo ya Ford ija?”—Mkonzi]. M’bale Carl! [“Chonde.”] Ayi. Iye akundiiza ine za ndakatulo yaing’ono imene ndinali nayo nthawi ina, ya Ford yanga. Si malo abwino kuti ndiyipereke iyo, M’bale Carl.

<sup>3</sup> Chotero, ndife oyamikira kwambiri. Ndipo ndinali ndi maumboni abwino ochuluka kwambiri mmawa uno, kumva kuchokera kwa abale awa, ndinakomana nawo ena a amunawo.

<sup>4</sup> Ndipo panali mtumiki amene wangoyankhula kumene pano, m’bale wamng’ono wachi Spanish amene anapereka yake. . . nthawi ya mnyamata wamng’ono kuti ayimbe. Kodi izo sizinali zodabwitsa kwa liwu la wa zaka sikisi zakubadwa? Mai, liwu labwino kwambiri limene ine ndinayamba ndalimvapo, la mnyamata wamng’ono wonga ameneyo.

<sup>5</sup> Tsopano, m’bale uyu, abale anayiwala zimenezo, koma iye ali ndi msonkhano kuno mu mzinda wanu. Ine ndikuganza ndi kumusi ku church of God, kapena Assemblies of God? [M’baleyo akuti, “Assemblies.”] Assemblies of God, kumusi ku Assemblies of God. Ndipo ndikutsimikiza kuti iwo angayamikire kwanu—kupezeka kwanu. Kodi msonkhanowo ukutenga nthawi yayitali bwanji, m’bale? [“Mpaka Lamlungu.”] Mpaka Lamlungu. [“Lamlungu usiku.”] Mpaka Lamlungu usiku. [“Tikakhala ndi kuyimba usikuuno.”] Bwana? [“Tikakhala ndi kuyimba usikuuno.”] Kuyimba usikuuno. Tsopano inu nonse mukuitanidwa kuti mubwere ku msonkhano umenewu. [“Pa hafu pasti seveni.”] Hafu pasti seveni, usikuuno. Ndipo kodi tchalitchicho chiri kuti, m’bale? [“113 West Clay.”] Kodi inu mungangotiuza ife kumene icho chiri? [“113 West Clay.”] 113 West Clay Street, komwe kuno mu mzinda wa Flagstaff. Ndipo—ndipo ndikutsimikiza kuti inu mu . . .

<sup>6</sup> Kodi mnyamata wamng’onoyo akakhala ndi inu? [M’baleyo akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Ayi, abambo ake akayimba. Inu mumaimba, sichoncho inu? Chabwino, izo nzabwino, ine ndimazipeza zimenezo molondola basi, kwa nthawi imodzi.

Chabwino, si kawirikawiri kuti umaziwona zimenezo; koma izo, kawirikawiri, ngati pali luso limodzi m’banjalo, zimatengera kuchokera—kuchokera kwa lina lonselo, ine ndikuganiza. Chotero iwo atero... [“Izo zonse zinayambira mu kusala ndi kupemphera, M’bale Branham.”] Kusala ndi kupemphera, tsopano ndizo—ndizo zabwino kwenikweni.

<sup>7</sup> Tsopano, inu mukudziwa, ngati Amerika, onse pamodzi, mabanja athu onse Achimerika akanakhala monga chomwecho, chabwino, iwo akanangowachotsapo apolisi onse. Zakachikwi zikanayambika, sichoncho izo? Ife tikanakhala mu kalasi yoyamba pamenepo. Uko nkulondola. Imfa yonse ikanazimirira, matenda onse, chisoni, zokhumudwitsa zonse, ndipo ife tikanakhala ndi Khristu.

<sup>8</sup> Chotero, ndife okondwa, ndipo ndikumva maumboni abwino onsewa! Ndipo ndinali ndi mwayi wokumana ndi M’bale Earl, kwa nthawi yanga yoyamba. Ndipo—ndipo usiku watha ine ndimayankhula ndi mkazi wake, ndipo—ndipo iye wakhala akutchulidwa ndi kuchiritsidwa, nthawi zingapo, mu misonkhano; anati, pa msonkhano wotsiriza iye anali pa nsanja.

<sup>9</sup> Chotero, zimatipangitsa ife pang’ono, kukhala ngati oseketsa pang’ono. Ine sindimamukumbukira M’bale Earl, ngakhale ine ndinali nditagwirana naye chanza penapake. Ndipo—ndipo ine ndinali nditakhala pa zenera, usiku watha, ndikumudikirira iye kuti abwere. Ndipo mwamuna wamtali wamkulu anabwera pamenepo, anali ndi masharubu akuda. Ine ndinati, “Apa iye akubwera.” Ndipo kenako pamene... Billy, mwana wanga, anati, “Oh, ayi,” anati, “ameneyo si M’bale Earl. Iye ndi wamng’ono kwambiri kuposa munthu ameneyo.” Ndipo chotero kenako ndinadzakumana ndi Mlongo Earl kuno usiku wathawu, ndipo ndinali ndi mwayi wokhala mnyumba yawo yokondeka kuno mu mzinda.

<sup>10</sup> Ano ndi malo abwino. Ine nthawizonse ndimafuna kuwatchesa iwo *flagpole* mmalo mwa Flagstaff, pamwamba pa phiri apa, mwaona. Ndipo, ine ndikukuzani inu, ngati pali aliynese pano wochokera ku Texas, tsopano inu mumabwekerera. Ine ndinachoka ku Tucson, dzulo, pafupifupi sevente-thuu kapena sevente-faivi, penapake cha pamenepo, ndipo pamwamba pano kuno mmawa uno ndavala chikhoto. Mwaona, zimene iwo ali nazo mu Texas, ife tiri nazo mu Arizona, sichoncho ife? Uko nkulondola. Ife tiri komwe kuno.

<sup>11</sup> Nthawi ino ya chiyanjano! Dokotala Bosworth Wokalamba, mzanga wa ine, ambiri a inu mwina mumamudziwa M’bale Bosworth. Iye anali mmodzi mwa okalamba opatulika kwambiri. Ndipo iye ananena kwa ine nthawi ina, iye anati, “M’bale Branham, inu mukudziwa chimene *chiyanjano* chiri?”

Ine ndinati, “Ine ndikuganiza chomwecho, M’bale Bosworth.”

<sup>12</sup> Anati, “Ndi anthu awiri mu chombo chimodzi, chotero iwo akuyenera kugawana pang’ono.”

<sup>13</sup> Chotero ndicho chimene chiyanjano chiri, timatenga ndi kupereka, kugawana wina ndi mzake; ndi M’bale Carl Williams, ena onse, M’bale Outlaw. Oh, mmodzi wa anthu oyambirira mu Arizona amene anayamba wathandizirapo umodzi wa misonkhano yanga, anali M’bale Jimmy Outlaw, ndipo ife takhala tiri abale apamtima kuyambira nthawi imeneyo. Ndipo ndife okondwa kwambiri chifukwa cha inu nonse, chifukwa cha atumiki ndi abale amene ife timakumana nawo kuno. Ine ndiribe nthawi yogwirana chanza ndi aliyense, monga ine ndimakonda kuchitira, koma chimakhala chiyanjano pamene ife tisonkhana limodzi.

<sup>14</sup> Zimangondikumbutsa ine za—za msonkhano waku Phoenix. Ine ndakhalapo nawo mwayi, kuyambira pamene machaputala anayamba, ku—kuthandizira kukonza machaputala ndikuyankhula mmenemo. Ndipo ndi bungwe lokhalo limene ine ndirimo, ndipo ilo si bungwe. Ndi chamoyo chogwira ntchito pakati pa anthu.

<sup>15</sup> Ndipo ngati ena a inu amuna muno mmawa uno, amene—amene simuli a chiyanjano ichi, cha Christian Business Men ichi, Full Gospel, mulole. . . ngati mumakhulupirira ndipo mutenga mawu anga, ndi limodzi la magulu abwino kwambiri a anthu. Ndipo—ndipo kwa abale otumikira, izo si zotsutsana ndi mpingo wanu, ndi za mpingo wanu. Mwaona, ndi njira yawo yokhazikitsiramo ku—ku mpingo.

<sup>16</sup> Ine ndinangopezeka ndikuyang’ana mozungulira pa dona wokonedwa uyu apa amene wangoyimba kumene nyimbo ija mphindi zingapo zapitazo. Ine ndamvapo kuyesera kochuluka kwa iyo, koma dona ameneyo anali ndi liwu lokwanitsa kuchita izo molondola, inu mukudziwa, mopanda kuifinya iyo, chomwecho. Ine ndinazikonda zimenezo kwambiri, dona, zinali zabwino, zabwino kwambiri. Anati anali mkazi wa mtumiki pano. Ndipo, m’bale, inu mukuyenera kuti iye azikuimbirani inu kuti mugone usiku uliwonse, chotero izo zingakhale zabwino kwambiri, zabwino kwambiri. Iko kunali kuyimba kwabwino kwambiri. Ine ndikuyamikira zimenezo.

<sup>17</sup> Ndipo, mmawa uno, izo zikukhala ngati zikundikumbutsa ine pang’ono za—nkhani yaying’ono. Kutu, ine—ine ndimakonda kusaka ndi kuwedza, ndipo ndicho chimodzi cha zifukwa zimene ine ndiri kuno mu Arizona, chotero, ndi kuyamba kusaka ndi kuwedza. Ndipo ine ndimakonda izo. Ndipo chotero ine ndinkawedza nthawi ina mu New Hampshire.

<sup>18</sup> Ndipo ndikuganiza ndiri ndi abwenzi ambiri muno amene amakonda kuwedza, awiri onse mwa amuna ndi akazi, nawonso, mwaona. Tonse timakonda izo.

<sup>19</sup> Chotero ine ndinali ndi hema wamng'ono amene ndinali nditayika pamwamba, pamwamba pamene, inu mukuwadziwa anyamatawo, kukhala ngati wolemera pang'ono kapena chinachake, sindimakhoza kuyenda pamenepo. Ndipo pamenepo panali zabwino zambiri, za izo, mphuta za mu mtsinje, ndi zabulauni, ntchira, anjolinjo. Oh, izo ndizodzaza, timitsinje tating'ono timeneto tikutsika kuchokera pamwamba pa mapiri mu New Hampshire. Ndi mphuta zazing'ono, mwinamwake ma inchesi fortini, kutalika ma inchesi sikisitini, zochuluka basi za izo! Ndipo ndimangokhoza... Ine ndimapita kumeneko ndi kukagwira izo, basi kungosangalatsidwa ndi kuziwedza izo, nkuzisiyanso. Ngati ndapha imodzi, ndiye ine—ine ndimakaidya iyo, inu mwaona, kuibweretsa iyo.

<sup>20</sup> Chotero ine ndinali ndi wina wa nsondodzi wa mphalapala wina wakale ukukula, ndipo—ndipo nthawi zonse ndimasintha chingwe chowedzera changa... Ine ndinali ndi cha Royal Coachman chaching'ono. Ndinkaponyeranso ndi chimenecho, ine ndikachisintho icho pamenepo panali mulu wa nsondodzi wa mphalapala. Ndipo ndinaganiza, “Chabwino, ndikatenga chikwanje ndipo ndipita kumeneko, mmawa uno, ndipo—ndipo ndikatchetcha nsondodzi wa mphalapala umenewo uko, kuti chingwe changa chisakakodwe pa izo.” Oh, ine ndinayang'ana mmbuyo panso pa lachikale laling'ono... ngati dziwe la kanyimbi laling'ono, ndipo iwo anali atangogona mmenemo, akungoyembekezera Coachman uja kuti afike pa iwo. Tsopano, usiku wonse... Ndinkakonda kunena kuti, “ndiri ndi tsitsi langa,” koma ndiribe tsitsi lokwanira kuti izo zingalowemo tsopano. Chotero ine ndinali... Ine basi... izo basi momwe izo—momwe iwo angadzayang'anire izo. Ndipo chotero ine ndinafika kumeneko, mmawa umenewo, ndinatenga chikwanje chaching'ono chakale ichi, ndipo ndinakadula nsondodzi wa mphalapala uwu. Ndipo ndinali nawo atatu kapena anayi, amapita kuti akakonze kadzutsa, ndi kubwereranso. Ndipo ine si wophika wabwino kwambiri. Ndipo chotero ndinamuuza mkazi wanga kuti sindingathe kuwiritsa madzi osawaphwetsa iwo, chotero inu mukudziwa kuti imeneyo ingakhale ntchito yoipa kwambiri yophika.

<sup>21</sup> Chotero, pa ulendo wanga wobwerera, apo panali mayi chimbalangondo wachikulire ndi ana awiri, ndipo iwo anali atalawa mu hema yanga yaying'ono. Ndipo inu mumakamba za kuphwasula chinachake, inu simukudziwa momwe zinthu zingaphwasuliridwe mpaka mutalola chimbalangondo chidzalowe muhema. Icho, si chimene icho chimaphwasula... chimene icho chimadya, ndikutanthauza, ndi chimene chimaphwasula. Ndinali ndi mbaula yaying'ono, mbaula yaying'ono iyi ya wolishya nkhusa, ndipo izo zimakwera pa mbaula yaying'ono iyi ndi kumangolumpha chokwera ndi chotsika, kuti zimve paipi ikuphokosera, ndi kungoyiphwanyana

iyu mu zidutswa, inu mukudziwa. Ndipo pamene ine ndinkabwera uko, ine ndinali ndi mfuti yaing'ono ya dzimbiri ya .22 ili pamenepo, koma ine ndinali ndi nkhwangwa iyi mdzanja langa.

<sup>22</sup> Ndipo, inu mukudziwa, pamene ine ndinabwera uko, mayi wokalambayo anathamangira kumbali imodzi, ndipo iye anafuulira kwa ana ake. Ndipo mwana mmodzi anatsatira, chabwino; koma winayo anakhala, kanthu kakang'ono kwambiri. Mu Meyi, inu mukudziwa, zimangotuluka. Nsana wake wonse unali utapendekera kwa ine, munga *choncho*. Ndipo ndinaganiza, “Kodi iye akuchita chiyani?” Chabwino, ndiye iye anadzayang'ana pa ine. Ndipo ndinkafunafuna mtengo, kuti ndingowona momwe—kufupikira kwake kunaliri, chifukwa izo zikhoza kukukanda iwe, inu mukudziwa, chifukwa cha anawo. Ndipo, izo, iwe sungathe kuzithamangitsira kunja kwa iyo pozilankhula, mwaona. Chotero ine ndinamuyang'ana mayi wokalambayo kwa kanthawi pang'ono, inu mukudziwa. Iye anapitiriza kufuula, ndi kumapanga phokoso, chinachake ngati mbalame. Iwe umayenera kudziwa momwe chimamvekera. Chotero iye anapitiriza kufuulira mwanayo, ndipo mwanayo samabwera.

<sup>23</sup> Chabwino, ine ndinaganizira za mfuti yanga. Ndipo ndinaganiza, “Ayi, ngati ndingathamangire uko ndi kukatenga mfutiyo, ngati ndingakawombere mayi wokalambayo, kusiya ana awiri amasiye mu thengo,” ndipo sindimafuna kukhala wolakwa pa izo. Ndipo, pambali pake, ukali wake, twente-thuu imeneyo ingakhale kuti ndi yaing'ono, inu mukudziwa. Ndipo nthawizina iyo siimawombera, ndimayenera kuyikhetemula katatu kapena kanayi kuti iwombere. Chotero ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndingokwera mu mtengo umenewo apo, ngati iye angayambe kubwera kuno. Ine ndikakwera mmwamba mu mtengowo, ndikukapeza mtengo waung'ono ndi kungowakwapula iwo pa mphuno.” Mphuno yawo ndi yofewa kwambiri. Ndipo iwo amangokuwa, kenako nkumapita kumusi, inu mukudziwa, ndipo iwo amakusiya iwe wekha. Chotero ndinaganiza, “Ine ndikwera mu mtengo umenewo.”

<sup>24</sup> Koma chidwi cha wamng'onoyo, oh, atakhala munga *chonchi*. Ndipo ine ndinaganiza, “Kodi iye akuchita chiyani?” Chotero ine ndinapitirira kuzembera, ndikumamuyang'ana iye, inu mukudziwa, ndikutalikira pang'ono, ndi kumayandikira ku mtengowo, chifukwa iye anakhala akufuulira kwa mwanayo. Chotero ine ndinapita patsogolo pang'ono, ndipo inu mukudziwa chimene kamwanako kanali katachita?

<sup>25</sup> Tsopano, ine ndimakonda zimimina, kapena mapanikeke, ine ndikukhulupirira inu mumazitcha izo, kunja kuno. Kumusi Kummwera, timazitcha izo zimimina. Ndipo ine sindimatha kuzipanga izo bwino kwambiri, koma ndikutsimikiza ndimachita bwino pakudya izo. Ndipo, inu mukudziwa, ine

ndinali wa Baptisti. Sindimakonda kukonkha; ine ndimakonda kuzibatiza izo kwenikweni, kuyika manyuchiwo pa izo. Chotero ine ndinali ndi chitini cha manyuchi, pafupifupi chotalika *chonchi*, chiri pamenepo, chidebe chaching'ono cha theka la galoni la zimimina zanga.

<sup>26</sup> Ndipo kanthu kakang'ono kameneko, inu mukudziwa, chimbalangondo chimakonda kutsekemera, mulimonse. Iye anali atasegula chidebe cha manyuchi chimenecho. Ndipo iye anali atakhala pamenepo ndi dzanja laling'ono limenelo pafupifupi kutambalala *choncho*. Ndipo iye anali atanyamula icho mmanja mwake, ndipo iye amangomenyetsa phazi lake laling'onolo pansu, ndi kumanyambita munga *choncho*, inu mukudziwa. Uko nkulondola. Ndipo iye amatha kunyambita lirime laling'ono limenelo. Ndipo ine ndinayamba...Ndipo ngati ine ndikanakhala ndi kamera, ine ndikanakonda ndikanaziwonetsa izo mmawa uno, kuti mungoziwona izo. Ndipo apo iye anali, akupondetsa phazi lake laling'ono pansu pamenepo, ndi kumanyambita munga *choncho*. Ndipo ine ndinakuwa, "Choka pamenepo," munga *choncho*. Ndipo iye sanandilabadire ine konse, ndipo ankangonyambita munga *choncho*. Iye anachikombeza chidebe chija, mwaona.

<sup>27</sup> Ndipo ine ndinafuula pa iye munga *choncho*, iye anatembenuka ndipo anandiyang'ana ine munga *choncho*. Iye sankatha kutsegula maso ake, iye anangodzaza ndi manyuchi, inu mukudziwa. Paliponse mmaso mwake, mimba yake yaying'ono, yodzaza ndi manyuchi momwe iye akanakhallira! Ndipo kenako, patapita kanthawi, iye anadzandima chammbali, nathamangira kwa amayi ake. Iwo anamupititsa iye mutchire ndipo anakayamba kumunyambita iye. Iwo ankachita mantha kukhala pa chidebecho, koma iwo ankamunyambita iye.

<sup>28</sup> Ndipo ine ndinati, "Ngati uwo si mtundu wa msonkhano wabwino, wachikale wa chipentekoste; kungodzaza ndi zinthu zabwino, zinthu zokoma, iwo amapita kunja uko, ndipo winawake amakanyambita kuchokera pamenepo. Umenewo ndi msonkhano weniweni wa chiyanjano. Tsopano ife tangobwera kumene munga *chonchi*, kuti tidzalowetse manja athu mu chidebe, aliyense wa ife, mpaka mu chigongono, kwa madalitso a Mulungu. Ndipo ine ndikutsimikiza inu mukazipeza zimenezo ku chitsitsimutso chimene chikuchitika uko ku Assemblies of God, chikuchitika kumusi uko tsopano. Ambuye akudalitseni inu.

<sup>29</sup> Ine ndinanana mu Phoenix, tsiku lina, pang'ono... Ndikukhulupirira kuti sizimveka mosinjirira, za nthabwala yaying'ono yokhudza mtumiki amene amapita ku nsanja mmawa uliwonse, kwa zaka twente, mwamphamvu, iye amakhoza kulalikirira maminiti twente, ndipo kenako nkumaliza, ndipo chotero iwo samatha kumvetisa chifukwa chimene izo zimakhallira. Ndipo chotero, mmawa wina, iye analalikirira

pafupifupi maora foro. Ndipo a—madikoni anamuyitananso iye, ndipo—ndipo anati, “Abusa, ife timakukondani inu kwenikweni.” Anati, “Ife—ife tikuganiza kuti mauthenga anu amakhala opambana.” Ndipo anati, “Ife tikudziwa, monga gulu la madikoni, ife takhala tikukuwonani inu ndi kukupatsani inu nthawi, ndendende maminiti twente Lamlungu lirilonse mmawa.” Ndipo anati, “Mmawa uno anali maora anayi.” Anati, “Ife sitikumvetsa basi.”

<sup>30</sup> Anati, “Ine ndikuuzani inu, abale.” Iye anati, “Mmawa uliwonse, ndikapita kukalalikira,” anati, “mukandiyitanira ine pa nsanja, Ndimafikira ndi kuyika kamodzi ka Kokulumunya ka Moyo aka pansu pa lirime langa. Ndipo,” anati, “mu maminiti twente, pamene Kokulumunya ka Moyo katha,” anati, “Ine—ine—ine ndimamaliza,” iye anati, “Ndimadziwa kuti ndi nthawi yoti ndiime.” Ndipo anati, “Chimene chinalakwitsa mmawa uno, ndinatenga batani.”

<sup>31</sup> Carl Williams, Jewel Rose, abale apamtima enieni ndi abwenzi anga, iwo anapita kumusi tsiku lina, ndipo anakatenga batani pafupifupi lalikulu *choncho*, kuti andipatse ine, ndipo, koma ine ndiribe ilo mmawa uno. Chotero, ndife okondwa kukhala pano.

<sup>32</sup> Tsopano, kodi aliyense muno akumudziwa Dokotala Lee Vayle? Ine sindikuganiza...mwina ayi. Iye anali mlaliki wa Baptisti, Dokotala wa Zaumulungu, ndipo iye ali ndi madigirii ake. Iye anali mphunzitsi wa ku sukulu ya sekondale, kuyamba ndi kuyamba, ndipo iye ndi wabwino kwambiri, mwamuna wophunzira. Ndipo matepi anga a *Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo*, ine ndinawatumiza iwo kwa iye, kuti akakonzere galamara. Chifukwa, chi Kentucky changa chakale “menya, alibe, ndi katenge, ndi nyamuka, ndi kukapeza,” izo sizichita bwino kwa anthu amene amawerenga mabukhuwo, chotero iye amandikonzera ine galamara. Ndiyeno, iye atamaliza, anazitumizanso izo kangapo, kuti akapeze mawu owonjezera. Chimene, bukhulo likusindikizidwa tsopano, patapita pafupifupi zaka zitatu kapena zinayi.

<sup>33</sup> Iye anandifunsa ine, iye anati, “Kodi ndingalembe bukhu, ndemanga zanga zokha?”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ziri bwino, M’bale Lee.” Ndipo ine ndinaganiza... .

<sup>34</sup> Kenako iye anati, “Ine ndikuwuzani inu chinachake.” Anati, “Iwo sakuyenera kugulitsidwa; kuperekedwa.”

Ine ndinati, “Chabwino, ndiye, ine ndikutsimikiza kuti izo ziri bwino.” Mukuona?

<sup>35</sup> Ndipo chotero iwo anali ndi chithandizo, cha pafupifupi anthu teni kuti azithandizira izo, zimene zinawatengera iwo pafupifupi madola fikitini handiredi, ine ndikuganiza, ine ndauzidwa, pa teni sauzande a iwo. Ndipo chotero ife—

tinawapeza iwo, iwo achoka kosindikizidwa masiku angapo apitawo, ndipo ife tinangotenga awiri kapena atatu, dzulo, ndipo Billy anawabweretsa iwo. Ndipo iwo—iwo aperekedwa. Tsopano, ine sindinaliwerengapo ilo, ine sindikudziwa chimene iye akunena. Koma ine...Izi ndi mwa chikhulupiriro. Koma ndikutsimikiza, ngati mungafune kukhala nalo, ngati mungatilembere ife, ilo lidzatumizidwa kwa inu, kwaulere. Mukuona? Ndipo ilo likutchedwa *Mneneri Wa Mzaka Zana Za Makumi Awiri*.

<sup>36</sup> Ndipo kenako ndinazindikira pa chithunzi apa, kutsogolo kwa bukhulo, ambiri a inu muli ndi chithunzi ichi, ndithudi, ndipo munachiwona Icho, pamenepo ndi pamene Mngelo wa Ambuye anajambulidwa ku Houston, Texas. Koma iwo anadulapo gawo la Icho.

<sup>37</sup> Ndiye ndikuwona apa kumbuyo. Ndipo ndi angati pano amene anayamba akhalapo mu umodzi wa misonkhano, tiyeni tiwone? Ine ndikuganiza pafupifupi nonse a inu mwakhalapo. Mumandimva ine ndikunena nthawi zambiri, “Mthunzi uwo wapachikika pa winawake.” Tsopano, mwaona, ngati inu mupanga neno, ndipo ilo si choonadi, Mulungu sadzakhala ndi chirichonse chochita ndi ilo. Inu mukudziwa Mulungu sagwirizana ndi mabodza, koma Iye amangoikira kumbuyo chimene chiri choona.

<sup>38</sup> Chotero pamene Iye anamuza Mose, pamene Iye anakomana naye kumbuyo uko mu chipululu, mu Lawi la Moto, kumbuyo mu chitsamba choyakacho. Ndiye pamene Iye anawatulutsa anthu aja, ndi amene anamutsatira Mose, pa ulendowo, ndiye Iye anatsikira pa Phiri la Sinai, Lawi la Moto lomwe lija, ndipo anatsimikizira kuti chimene Mose anali atanena chinali choonadi.

<sup>39</sup> Tsopano, Mulungu adzachita izo. Iye nthawizonse amachita zimenezo. Chotero Kuwala uku *apa*, ndithudi, ife timakuyanjanitsa Iko ndi Mulungu, chifukwa Iko kuli ndi chikhaliidwe chomwecho ndi chirichonse chimene Iye anachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi.

<sup>40</sup> Ndiye pa izo, kumati, “Munthu uyu apa, ine ndikuwona iwe waphimbidwa ndi imfa, mthunzi wakuda.” Ndi angati, ambiri a inu munamvapo izo zikunenedwa! Chabwino, kuno posachedwapa mu msonkhano, kunali winawake wofuna kudziwa, ankafuna kuti awone ngati iwo akanatha kujambula chithunzi cha izo, pamene Izo zinanenedwa. Chotero iwo... Panali dona atakhala pafupi, ndipo bambo uyu anali ndi kamera. Ndipo ine ndinati, “Dona uyu wakhala apa, ndi Akazi a *Akuti-ndi-akuti*,” chirichonse chimene chiri. Ine ndinati, “Iye waphimbidwa ndi mthunzi wa imfa, koma iye ali ndi khansa.” Ndipo pomwepo iye anajambula chithunzicho, chifukwa izo zinali pafupi. Ndipo apo icho chinali, mwaona, mthunzi wa



khansa, yakuda ija ya imfa ikulendewera pa mkaziyo. Ndipo kenako Mzimu Woyera unayankhula mobwezera kenanso. . .

<sup>41</sup> Tsopano, pamene iwo anayika izi mu bukhu, iwo anazidula izo, chotero iwo anangoyika izi mkati muno basi mpaka iwo atapanga kusindikiza kwina kwa bukhulo. Ndipo ndi chifukwa chake muwona tsamba lomatuka limenelo pamenepo. Ndikuganiza kuti a *The Voice Of Healing* ndi omwe anasindikiza bukhulo.

<sup>42</sup> Ndipo tsopano ilo ndi la ulele mwamtheradi. Ndipo othandizira kumbuyo kuno kuseri kwa bukhuli, amene anaikamo madola fiftini handiredi mmenemo, kuti alifikitse ilo kwa anthu, kuti anthu akaliwerenge ilo. Chotero, ilo ndi laulere, ndipo ndi bukhu laling'ono labwino. Ndipo ine sindikudziwa zimene ziri mkatimo, sindinaliwerengepo; Atate akudziwa zimenezo.

<sup>43</sup> Koma mwaona, Icho chinali, kwa ine, Icho ndi mwamtheradi Choonadi. Ndicho chimene tikuchifunafuna, ndi Choonadi. Yesu anati, “Mudzadziwa Choonadi, Choonadi chidzakumasulani inu.” Ndipo Iye ndi Choonadi chimenecho. Iye ali, Yesu, Mwana wa Mulungu, ndi Choonadi cha Mawu, chifukwa Iye anali Mawu atasandulika thupi. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Kenako, izo zinamupanga Iye Choonadi, chifukwa Mawu ndi Choonadi, ndipo Iye anali Choonadi.

<sup>44</sup> Tsopano pamene ife tikumuona Iye akubwerera mmasiku otsiriza ano, kusuntha kwakukulu uku kwa Mulungu, kusuntha kudutsa mafuko a mdziko, kusonkhanitsa anthu kwa Mkwatibwi, icho ndi Choonadi.

<sup>45</sup> Zaka zapitazo, iwo anati, “Panalibe chinthu choterocho monga kuyankhula mmalirime. Zinali zamkutu.” Mulungu analonjeza izo, ndipo Iye anatsimikizira izo kuti ndi Choonadi. Uko nkulondola.

<sup>46</sup> Winawake anati, mmawa uno, ine ndikukhulupirira anali mlongo wathu wolemekezeka kumeneko amene amachita ndi ana kwambiri za ubatizo wawo, iye anati, “Inu mukhoza kumumva wina akuyankhula mmalirime. Koma, kumumva winawake akuyimba mmalirime, mwaona, icho chinali chinthu chokongola kwambiri.”

<sup>47</sup> Ndikukumbukira chondichitikira changa choyamba ndinali ku Rediger Tabernacle ku Fort Wayne, Indiana. Ndipo ine ndinali kuyankhula, ndinali ndi msonkhano wa machiritso, itachitika imfa ya—ya M'bale B. E. Rediger. Ndipo M'bale Bosworth anali ali kumeneko, Paul Rader. Ndipo ambiri a inu amuna akale, ngati ine, inu mukukumbukira Paul Rader; ndipo iye anali wa Baptist, ndipo ife tinali, chotero ife tinali abwenzi opambana. Ndipo chotero ndikuyankhula kumeneko,

ndimapita kukawapempherera odwala. Icho chinali chinthu chachilendo kwa iwo pamenepo. Koma dona anabweretsa mnyamata wamng'ono, amene anali wolumala, ndipo, pamene iye ankabwera kudutsa pa nsanja, masomphenya a Ambuye anawonekera ndipo anamuuza iye zonse za chimene chinali vuto ndi mnyamata wamng'onoyo. Ndipo ndinamupempha mtsikanayo kuti andipatsire—kuti andipatsire ine mwanayo.

<sup>48</sup> Tsopano chifukwa cha umboni wa mlongoyo, kuti muthe kuwona chisangalalo ndi chimene chiri chochitika chenicheni cha—cha chisomo cha Mulungu, chimene Iwo akanachita, pamene Icho chinagwira ntchito molingana ndi Mawu a Mulungu, mwaona, lonjezo la Mulungu la orali.

<sup>49</sup> Tsopano, lonjezo la Mulungu kwa Nowa silingagwire ntchito kwa ife lero. Lonjezo la Mulungu kwa—kwa Mose, ife sitikanakhala ndi Uthenga wa Mose. Mose sakanakhala ndi uthenga wa Nowa. Ife tiri ndi Uthenga wa ora. Ife sitikanakhala ndi uthenga wa Luther. Ife sitikanakhala ndi uthenga wa Wesley. Ino ndi nthawi ina. Mulungu anapereka Mawu Ake kwa m'badwo uliwonse. Ndipo pamene m'badwo umenewo ukubwera, Iye amamutuma winawake kumeneko kuti akatsimikizire Mawu amenewo, kuti akatsimikizire kuti izo ndi zoon. Ndipo tsopano ife tikuwona mu chirichonse ndiye, monga chimene Yesu ananena pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anati, “Inu mumamanga manda a aneneri, ndipo makolo anu anawaikamo iwo mmenemo.”

<sup>50</sup> Tsopano, anthu anga ndi Achikatolika, monga inu mukudziwa, pokhala wachi Irish. Tsopano ife... Tsopano iwo—iwo amakamba za Patrick Woyera, Akatolika amamunena iye. Chabwino, iye ndi wa Chikatolika mochulukha monga ine ndiriri. Iwo amayankhula za Joan waku Arc. Iwo anamuwotcha mtsikana ameneyo pa nkuni, ngati mfiti, ife tonse tikudziwa zimenezo, chifukwa iye anali wauzimu ndipo ankawona masomphenya. Ndithudi, zaka mahandirede zingapo zitatha, iwo anadzafukula thupi la ansembe amenewo, ndipo anachita kudzitunduza, ndipo anawaponyera iwo mu mtsinje. Koma izo si zomwe zimatengera, mwaona.

<sup>51</sup> Iwo nthawizonse amachiphonya icho. Munthu nthawizonse amamutamanda Mulungu chifukwa cha zomwe Iye anachita, kumayembekezera chimene Iye ati adzakhale, ndipo nkumanyalanyaza chimene Iye akuchita. Chimenecho ndi chikhalidwe cha munthu basi. Ndipo iye sanasinthe chikhalidwe chake, munthu wa mdziko.

<sup>52</sup> Chotero ife tikupeza kuti Uthenga wathu ndi, lero, Uthenga umene ife tiri nawo, wa, “Tulukani mu Babulo, ndipo mukhale amfulu, ndipo—ndipo mudzazidwe ndi Mzimu, ndi nyali zanu zikonzedwe ndipo ziziwala, ndipo, muyang'ane mmwamba, chiwombolo chathu chayandikira,” zinthu izi ndi zachirendo

kwa anthu ambiri amene amapuma ndi kutchula Dzina la Ambuye wathu wokondedwa.

<sup>53</sup> Komabe pakati pa zonsezo, ife tiribe kanthu kotsutsa anthu amenewo, anthu achipembedzo amenewo. Iwo onse ndi abwino, iwo ndi abwino. Iwo ndi athu—iwo ndi oyanjana nawo mu Uthenga, chifukwa Yesu anati, “Palibe munthu angabwere kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka iye. Ndipo—ndipo onse amene Atate andipatsa Ine, iwo azadza.”

<sup>54</sup> Chotero, ife tiri ndi udindo wofesa Mbewu basi. Zina zinagwera m’mbali mwa njira, zina mitundu yosiyanasiyana ya nthaka, zina zinadzagwera ndi kubereka mahandirede. Chotero, ife tangokhala ofesa Mbewu. Mulungu ndi Amene amailondolera Iyo pamene Iyo ikugwa. Ndipo tsopano ife tikupemphera kuti mwinamwake, mmawa uno, pakhale Mbewu yaing’ono itagwetsedwe penapake, imene ikhoza kumulimbikitsa winawake. Ndipo basi a—a—munthu. . .

<sup>55</sup> Kuti nditsirizitse umboni wanga wokhudza dona wamng’ono amene ine ndimati ndikambe za iye. Dona uyu anamubweretsa mwana wamng’ono uyu, mnyamata wamng’ono, ine ndikuganiza, pafupifupi usinkhu wa zaka teni, thwelofu, ndipo mwinamwake osati wamkulu chomwecho, chifukwa mkazi uyu anali atamunyamula iye. Ndipo iye anadzamupereka iye. Ndipo pomwepo, pamene ine ndinali kumupempherera mwanayo, mnyamata wamng’onoyo analumpha kuchokera mmanja mwanga ndipo anapita akuthamanga pansu pa nsanja, anthu pafupifupi sarte faivi handirede kapena foro sauzande. Ndipo pamene iwo anatero, chinthu choyamba chimene iwo anayamba achiwonapo chikuchitidwa, mayiyo, atakhala pa mpando wapatsogolo, anangokomoka ndi kugwa. Ndipo mtsikana wamng’ono wachi Amishi. . .

<sup>56</sup> Kodi inu mumawadziwa achi Amishi? Sindikudziwa ngati muli nawo kunja kuno, a tsitsi lalitali, iwo ndi anthu okoma kwambiri, ndi a ukhondo kwambiri komanso mtundu wabwino. Inu mukudziwa, mwa Amennonite onse, kapena Achiamishi, ndi ena otero, ife sitinakhalepo ndi mbiri imodzi ya ana olekerera. Atchuleni iwo oseketsa ngati mukufuna kutero, koma ife—ife tiri ndi chinachake chikusowekera mnyumba zathu, chimene iwo ali nacho. Iwo alibe mbiri imodzi mmakhoti, ya—ya khalidwe loyipa la ana likubwera pakati pawo. Iwo amawalera ana awo, mwanjira imodzi yokha, ndipo umo ndi momwe iwo amachitira.

<sup>57</sup> Ndipo dona wamng’ono uyu anali woyimba limba wotchuka, mkazi wamng’ono wokongola, ndi tsitsi lalitali, la mzindo litakhazikika kumbuyo. Ndipo pamene iye anayang’ana kutsidya. . . Tsopano, iye anali wachi Amishi, iye sankadziwa kanthu za Pentekoste, ndipo ngakhale ine sindinkadziwa. Koma pamene iye anayang’ana pa nsanja, ndi kumuwona

mnyamata wamng’ono akupita, akuyenda kudutsa pamenepo, iye anakweza mmwamba manja ake.

<sup>58</sup> Tsopano, ine ndikudziwa kuti pali kutengeka, ndipo ine ndikuyembekeza ine sindiri wokhudzidwa. Ine—ine sindine wabodza. Ndipo ine—ine sindiri. Ngati ndikulakwitsa, ine—sindikulakwitsa mwadala, ndikulakwitsa mosadziwa.

<sup>59</sup> Koma mtsikana ameneyo anaponyera manja ake mmwamba, ndipo tsitsi limenelo linagwera pansi pamapewa ake, ndipo iye anayamba kuyimba mu lirime losadziwika. Ndipo iye ankasewera nyimbo ija, “Sing’anga Wamkulu tsopano ali pafupi, Yesu wachifundoyo.” Ndipo pamene anadzalumpha kuchokera pamenepo. . . Ine ndikudziwa kuti izi zikumveka zachirendo tsopano. Koma mtsikana uyu anali asanadziwe kalikonse za kuyankhula mmalirime, koma iye amayimba mu malirime osadziwika, “Sing’anga Wamkulu tsopano ali pafupi, Yesu wachifundoyo.” Ndipo limba limenelo limapitirira kumayimba, “Sing’anga Wamkulu tsopano ali pafupi, Yesu wachifundoyo.” Chabwino, iwo anawunjika maguwa amenewo, ndipo pansi kudutsa pakhonde, mpaka pansi, anthu akukuwa! Mtsikana ameneyo atayima pamenepo, ndi nkhope yake mmwamba monga *choncho*, akuyankhula mu malirime ena; ndipo, limba, makiyi a nyanga ya njovu akuyendabe:

Sing’anga Wamkulu tsopano ali pafupi,  
Yesu wachifundoyo,  
Iye amayankhula ndi mitima yolefuka kuti  
isangalale,  
Palibe Dzina lina koma Yesu.

<sup>60</sup> Oh! Ndi. . . “Diso silinawonepo, ndipo khutu silinamvepo, chimene chasungidwira kwa ife.” Mukudziwa chimene ine ndikuganiza? Chifukwa chiyani—chifukwa chiyani kuti ife tivomereze cholowa mmalo kapena chinachake chimene chiri chodzipangitsa kukhulupirira, pamene miyamba ili yodzaza ndi zenizeni, Mphamvu yeniyeni ya Mulungu, imene ingamasule moyo, imene ingatichitire ife chinachake? Mulungu akudalitseni. Tsopano, pali zinthu zambiri.

<sup>61</sup> Ine sindinakuuzeni inu kumene mungakalipeze bukhu ili, mwaona. Post Office Box 325, ku Jeffersonville. Ndipo ngati inu mungawalembere, bwanji, iwo angalitumize ilo kwa inu. Kapena, mwina, mudzachezere umodzi wa misonkhanoyo, iwo adzakhala akupereka iwo.

<sup>62</sup> Tsopano, ndine woyamikira kwambiri chifukwa cha nthawi yabwino iyi ya chyanjano. Ndipo mmawa uno ine ndimaganiza za nkhani yaing’ono imene ine ndinkakonda kuyinena kwa a Christian Business Men, ya Zakeyu. Ambiri a inu mwandimvapo ine ndikunena iyo, za momwe munthu wamng’ono uyu sankakhulupirira zozindikira zamumtima izi, ndi, za Ambuye. Chifukwa, ine ndikuganiza, monga ife timakhala nazo mu

m'badwo uliwonse, inu mumawona chenicheni, kenako inu mumawona chokopera. Ndipo ife timayenera kungopirira nazo izo. Koma abwino, oganiza molimba ndi amuna Mwamalemba amamvetisa, mwaona. Chimene, ife, ndipo ziribe kanthu. . .

<sup>63</sup> Pamene Akazi a Aimee Semple McPherson, pamene iye anali kuno pa dziko lapansi, mu utumiki wake, amanena kuti pafupifupi mlaliki wamkazi aliyense ankavala mapiko amenewo, monga, inu mukudziwa, kapena mikanjo monga choncho, ndipo ankanyamula Baibulo.

<sup>64</sup> Tangoyang'anani pa a Billy Graham ali mdziko lero. Koma, inu mukudziwa, Billy Graham sangathe kutenga malo anu. Ine sindingathe kutenga malo a Billy, iye sangathe kutenga anga. Ine sindingathe kutenga anu, ndipo inunso simungathe kutenga anga. Ndinu munthu payekha, mwa Mulungu. Mulungu anakupangani inu momwe inu muliri, kwa cholinga china. Ngati ife tikanangopeza malo athu, ndiyeno nkukhala pamenepo. Ngati ife tiyesera kuchita chinachake chosiyana, ndiye, mwaona, ndife—ife tiri mu dera la munthu winawake, zimene timangowononga chithunzi cha Mulungu.

<sup>65</sup> Ife timutenge ngati Billy Graham mdziko lachipembedzo lero, monga iye aliri, ngati tingatchule izo mwina kwa wosewera mpira, iye ali ndi mpirawo.

<sup>66</sup> Tsopano ngati muyesera kulanda mpira kuchokera kwa munthu wanu yemwe, mukungosokoneza timu yanuyo. Mtetezereni munthu wanuyo, mwaona. Muzipitiriza kumutetezera iye, asungeni ena onsewo kuti iye athe kuthamanga. Ndipo tidzakhala ndi kugoletsa pakapita kanthawi, ndipo Yesu adzabwera, ndipo kenako zonse zidzakhala zitatha. Ambuye akudalitseni inu.

<sup>67</sup> Tsopano ndikhala ndikukamba za munthu uyu, Zakeyu. Ndipo ine ndinali naye iye ali mmwamba mu mtengo uwu, inu mukudziwa, ndi masamba atakokedwa momuzungulira iye. Ndipo kenako pamene iye anadzatsika mu mtengom, iye anapita kwawo ndi Yesu. Ndipo ine ndinati, "Iye anadzakhala membala wa gawo la Full Gospel Business Men." Chotero ngati alipo a Zakeyu aliwonse pano, mmawa uno, ine ndikuyembekeza kuti inu mutenga langizo labwino limenelo ndi kukhala membala wa Full Gospel Business Men.

Inu mukuti, "Full Gospel?" Inde, bwana.

<sup>68</sup> Ndi chinthu chokhacho chimene Yesu akanati azilalikira, ukanakhala Uthenga wathunthu. Uko nkulondola. Kodi si kulondola uko? Ndithudi, pakuti Iye anali Uthenga wathunthu. Uko nkulondola. Iye sakanatha kudzikana Yekha.

<sup>69</sup> Koma tsopano ine ndiri ndi Malemba angapo omwe ndawalemba apa, a mutu waung'ono, wodziwika waung'ono, sizinditengera ine koma mphindi zochepe chabe, ngati inu mungapirire nane ine. Ndipo tisanachite ichi. . . Tsopano, mu

chiyanjano chathu chaching'ono cha kusunkhana pamodzi, ndi kuyankhula za manja a chimbalangondo, mu chidebe, ndi zina zotero, tsopano tiyeni tingosiya pambali zonse izi tsopano, ndipo tingoganiza kuti tikudziwana. Ndipo, ndipo tikufuna tsopano kuti tilowe mu gawo lakuya la Mawu.

<sup>70</sup> Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano, pamene ife tikuyandikira Iwo. Chifukwa, tiribe ufulu kuti tiwafikire Mawu, popanda kuyankhula ndi Mlembi, choyamba.

<sup>71</sup> Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, maso athu otsekedwa, ndipo ine ndikudalira kuti mitima yathu yaweramitsidwa ndi mitu yathu. Ine ndikudabwa, pamene ine ndikukweza maso anga ndi kuyang'ana pa omvetsera, ngati pangakhale winawake pano amene angati, pokweza manja awo, “M'bale, mtumiki, ndikumbukireni ine mu pemphero. Ndine—ndine wosowa lero”? Mulungu akudalitseni. Mulungu akudalitseni. Tsopano Iye akuwona dzanja lanu. Iye akudziwa chimene chiri pansu pa dzanja lanu, mu mtima mwanu. Mulole Iye apereke icho, ndiro pemphero langa.

<sup>72</sup> Wokonedwa Mulungu, pamene ife tiri oyamikira chifukwa cha nyumba iyi imene ife, ana Anu odzichepetsa, tikhoza kudzisonkhanitsa tokha pamodzi pansu pano, ndi kudzangoyankhula ndi kukhala ndi chiyanjano, kuti tidzangokhala ifeeni, pamene tikudzipeka tokha kwa Khristu, ndi kukhumba kukhala monga Iye. Ife ndi abale otumikira akhala pafupi, Ambuye, amuna amene ali okhoza mochulukira kuyima pano kuti apereke Mawu awa kuposa ine, kapolo Wanu wosayenera, koma izo zagwera pa ine. Ndipo, Atate, ine ndikupemphera, lero, kuti ngati ine ndinganene chinachake chimene sichingakhale cholungama molingana ndi chifuniro cha Mulungu, kuti, ndisanachinene icho, Mutseke pakamwa panga; monga Inu munachitira pakamwa pa mikango, tsiku lina, kuti iyo isamuvutitse Daniele.

<sup>73</sup> Atate, ife tikukupemphani Inu tsopano kuti mumukumbukire aliyense, mtumiki aliyense. Ndipo chitsitsimitso ichi chimene chikuchitika muno mu mzinda, Ambuye, mpaka ku Assemblies of God, ine ndikupemphera, Mulungu wokonedwa, kuti Inu mutumize chitsitsimitso chotero mmenemo kuti mzinda wonse uno ugwedezeke ndi Mphamvu ya Mulungu, kuti ma bala onsewa ndi ana oyendayenda mu msewu abweretsedwe ku Mpando wachifumu wa Mulungu, ndi kudzazidwa ndi ubwino Wake ndi Mzimu Wake. Perekani izi, Atate Akumwamba.

<sup>74</sup> Ndipo ife tikupemphera kuti lero, kuti ngati pangakhale mwamuna kapena mkazi, mnyamata kapena mtsikana, amene wabweretsedwa mu msonkhano uno mmawa uno, pano pansu pa chitetezero ku chipale chofewa, kuti Mzimu Woyera waukulu uyendere mitima yawo ndi kuyankhula kwa iwo, mwanjira

yachinsinsi. Mwinamwake ena amene anasochera, amene nthawiina anakucherezanipo Inu, Ambuye, koma tsopano anachokapo; abwezeretseni iwo, Ambuye, mmawa uno.

<sup>75</sup> Ndipo tikupempherera chaputala ichi, M'bale Earl ndi mkazi wake, ndi enawo. Perekani izi, Ambuye.

<sup>76</sup> Tsopano nyemani kwa ife Mkate wa Moyo, pamene ife tikutsegulanso masamba a Mawu, chifukwa ife tikudziwa kuti Baibulo liribe kutanthauzira kwa mseri. Koma, Mulungu sasowa kuti ife tizitanthauzira Mawu Ake, Iye ndi wodzitanthauzira Yekha. Iye ananena tsiku lina, “Pakhale kuwala,” ndipo panali kuwala. Iye anati, “Namwali adzaima,” ndipo iye anatero. “Ndipo mmasiku otsiriza Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa thupi lonse,” ziribe kanthu chimene dziko linanena, Iye anachita izo. Iye samasowa wotanthauzira. Iye amatanthauzira Mawu Ake Omwe, powapanga Iwo kukhala amoyo ndi kuwatsimikizira Iwo kuti ali chomwecho. Bwerani ku mitima yathu, Ambuye Yesu, ndipo mudzatanthauzire kwa ife, lero, zinthu zimene ife tikuzisowa. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>77</sup> Tsopano mu Baibulo, ngati inu mungatsegule. Ine ndikukhulupirira ine sindinayambe ndakhalapo ndi uthenga umene ine ndimayesera kuti ndiyankhulepo, umene ine sindinayambe ndawerengapo Mawu. Chifukwa, mawu anga adzalephera, ndine munthu. Koma Mawu Ake sangalephere basi, Iye ndi Mulungu. Chotero tiyeni titsegule tsopano kwa mutu waung'ono, ndipo ife tituluka mu pafupifupi sarte, maminiti forte, Ambuye akalola.

<sup>78</sup> Pa Chivumbulutso tsopano, ife tikufuna kuti titsegule ku mutu wa 3 wa Chivumbulutso, kuyambira ndime ya 14. Ndipo ife tikufuna kuti tiwerenge gawo chabe, ndi Uthenga kwa M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Ndipo ine ndikukhulupirira, ndipo ine—ine ndikuganiza pafupifupi anthu onse odzazidwa ndi Mzimu ndi owerenga Baibulo amakhulupirira, akhoza kunena *ameni* kwa izo, kuti ife tiri mu M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya, chifukwa umenewo ndi m'badwo wotsiriza. Mvetserani ku Uthenga wa chikhalidwe cha mpingo pa nthawi ino.

*Ndipo kwa mngelo wa Mpingo wa...Laodikaya lemba; Zinthu izi anena Amen, mboni yokhulupirika ndi yoona, chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu;*

*Ndikudziwa ntchito zako...iwe si wozizira kapena wotentha: ndikanakonda kuti ukanakhala wozizira kapena wotentha.*

*Chotero ndiye chifukwa iwe ndi wofunda, ndipo osati wozizira kapena wotentha, ine ndidzakulavula iwe kuchoka mkamwa mwanga.*

*Chifukwa iwe ukuti, ine ndi wolemara, ndi wochulukidwa mu katundu, ndipo wosasowa kanthu;*

*ndipo sudziwa kuti ndiwe watsoka, . . . womvetsa chisoni, . . . wosauka, . . . wakhungu, ndi wamaliseche:*

*Ndikulangiza iwe kuti ugule kwa ine golide woyesedwa mu . . . moto, kuti iwe ukhale wolemera; ndi zovala zoyera, kuti iwe uvale, ndi kuti manyazi a umaliseche wako asawonekere; ndi kudzoza maso ako ndi mankhwala a mmaso, kuti iwe uthe kupenya.*

*Onse amene Ine ndiwakonda, Ine ndimawadzudzula ndi kuwawapula: khala wachangu chotero, ndipo ulape.*

*Taona, ndayima pakhomo, ndipo ndikugogoda: ngati wina amva mawu anga, ndipo ndikutsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi ine.*

*Kwa iye amene agonjetsa ine ndidzamulola kuti adzakhale ndi ine mu mpando wanga, monga Inenso ndinagonjetsa, ndipo ndakhala pansu ndi Atate anga pa mpando wachifumu wake.*

*Iye amene ali ndi khutu, muloleni iye amve chimene Mzimu ukunena kwa mipingo.*

<sup>79</sup> Ambuye adalitse kuwerenga kwa Mawu awa. Tsopano ndikufuna kuti nditenge, kwa mphindi pang'ono chabe, mutu waung'ono, wotchedwa, *Zitseko Mu Chitseko. Zitseko Mu Chitseko*. Tsopano ichi ndi kwambiri. . . *Zitseko Mu Chitseko*, ndi mawu atatu. *Zitseko Mu Chitseko*.

<sup>80</sup> Mukhoza kunena kwa ine, “M'bale, mwina pali anthu handirede pano. Pamenepo, kodi simukuganiza kuti iwo ndi mutu wawung'ono, pamene muli ndi miyoyo handirede patsogolo panu?”

<sup>81</sup> Chabwino, izo, izo zikhoza kukhala zoono, a—mutuwo ndi wawung'ono. Koma si kukula kwa mutuwo, kumene—kumene kumawerengedwa, ndi chimene iwo uli. Ndi—ndi chimene lemba likunena, kumene kumawerengedwa.

<sup>82</sup> Monga, ine ndikukhulupirira munali mu Louisville, Kentucky, nthawi ina kalelo, a—mnyamata wamng'ono anali mchipinda chapamwamba, akusewera ndi bokosi losungiramo zinthu lakale mmwambamo, ndipo iye anapeza sitampu yachikale. Chabwino, chinthu choyambirira mmalingaliro ake, iye akhoza kukagula ayisikirimu pa iyo. Kunali wotolera kumusi mu msewu, chotero iye ananyamuka kupita kumusi mumsewu, mwamphamvu momwe akanapitira. Ndipo anati, “Mundipatsa chiyani pa sitampu iyi?”

<sup>83</sup> Wotolerayo anayang'ana pa iyo, ndipo inali ngati yofufutika. Iye anati, “Ndikupatsa iwe dolla.”

<sup>84</sup> Mai, iyo inagulitsidwa mosavuta. Iye akanalola iyo kuti ipite pa mtengo wa faivi senti, ndipo kenako nkukhala wokondwa



nazo izo, kuti akapeze ayisikirimu, koma iyo inagulitsidwa dolla. Wotolerayo anayigulitsa iyo madolla faivi handiredede. Ndipo kenako, ine sindikudziwa kumene iyo inapita, iyo inapita ku mahandiredede a madolla. Inu mwaona, ka pepala kakang'onoko sikanali kakakulu kwambiri, kachidutswa chabe kamene inu simungakatole pansi. Koma, silinali pepalalo limene linkawerengedwa, ndi chimene chinali pa pepalapo, chimene chimawerengedwa.

<sup>85</sup> Ndipo umo ndi momwe zimakhalira ndi kuwerenga Mawu a Mulungu. Si pepala lokhalo, mtengo wa pepalalo, kapena kukula kwa pepalalo, ndi zimene zalembedwa pa pepalalo. Ndipo mawu amodzi ndi okwanira kuti apulumutse dziko, ngati iwo angalandiridwe mwanjira imeneyo.

<sup>86</sup> Nthawi ina kale kunali . . . Ndinawerenga nkhani ya masiku a olemekazeka athu . . . Mmodzi wa Mapurezidenti aakulu amene ine ndikuganiza fuko linayamba lakhalapo nawo anali—anali Lincoln. Osati chifukwa chakuti iye ankachokera ku Kentucky, koma chifukwa chakuti iye anali munthu wamkulu. Iye anamanidwa maphunziro, komabe panali—panali chinachake mu mtima mwake, cholinga china.

<sup>87</sup> Ine—ine ndimakonda munthu wa masomphenya. Ndimakonda anthu amene amakhala ndi chinachake chimene akuchimenyera, osati kungogona mozungulira, “Chabwino, chirichonse chimene chingabwere zikhala bwino.” Oh, kumadzuka ndi kumachita chofunikiracho! Ndipo Lincoln sanalole konse maphunziro ake ayime panjira; iye anali ndi chinachake choti achite. Ine ndikuganiza Mkristu aliyense akuyenera kukhala mwanjira imeneyo, mupeze cholinga chanu ndipo mupite mukachichite icho.

<sup>88</sup> Membala aliyense wa chaputala ichi, osati, “Chabwino, timakhala ndi kadzutsa kamodzi pa mwezi,” si zimenezo, “kapena kamodzi Loweruka lililonse.” Muzikhala ndi cholinga mwoyo, chinachake chimene muti mudzachite. Tiyeni. Mulungu wakuyikani inu kuno; muzichita chinachake pa izo, membala aliyense wa mpingo uliwonse. Muli chitsitsimutso mtawuni. Chitsitsimutso chimenecho chiri kumeneko kwa cholinga. Tiyeni tikatengepo chinachake mu icho. Tiyeni tikachitepo chinachake pa icho.

<sup>89</sup> Bambo Lincoln. Kunali munthu amene . . . mnyamata wamng'ono, iye—iye anali mu nkondo, ndipo—ndipo iye anali—iye anali wamantha, kuyamba ndi kuyamba. Ndipo pa nthawi ya ntchito, iye—iye—iye anachoka pa ntchito yake; ndipo iwo anapeza chinachake chomutsutsa iye, kuti iye ankayenera kuti adzawomberedwe. Ndipo, oh, iye . . . izo zinali zoipa. Ndipo mnyamata mmodzi wamng'ono ankamukonda iye kwambiri, anapita kwa Bambo Lincoln, kuti akapemphe chikhululukiro.

Iye anali Purezidenti pa nthawiyo, mu United States kuno, ndipo chotero iye anapita kwa iye kuti akamukhululukire.

<sup>90</sup> Ndipo anati kwa iye, pamene iye ankatuluka mu galeta wake; ndi Bambo Lincoln, wamtali, wandevu, wakummwera kwenikweni, wochepa thupi. Ndipo iye anati, “Bambo Lincoln, pali mnyamata amene ati afe, mmasiku awiri kuchokera pano, adzawomberedwa, chifukwa iye anathawa mu nthawi ya nkondo.” Ndipo iye anati, “Bambo Lincoln, mnyamatayo si mnyamata woipa. Koma mifuti yonseyo ikuwombera, ndi—ndipo anthu akufa, iye anali wamanjenje. Ndipo anasokonezeka kwambiri, mwakuti, iye anakweza manja ake mmwamba ndipo anayamba kukuwa.” Iye anathamanga, anati, “Ine ndikumudziwa mnyamatayo.” Anati, “Bambo Lincoln, dzina lanu lokha pa pepala ili lingamupulumutse iye. Kodi inu muchita zimenezo?”

<sup>91</sup> Ndithudi, njonda ya Chikhristu iyi, mwachangu inasayina pepalalo, “Ndamukhululukira, *Wakuti-ndi-wakuti*.” Anasayina dzina lake, “Abraham Lincoln, Purezidenti wa United States.”

<sup>92</sup> Anabwerera mtumikiyo mwamphamvu momwe akanathera. Ndipo anathamangira ku chitokosi, iye anati, “Ndiwe mfulu! Ndiwe mfulu! Apa pali ya Bambo Lincoln, siginecha ya Bambo Lincoln. Ndiwe mfulu!”

<sup>93</sup> Iye anati, “Iwe ungabwere bwanji kudzandisereula ine, ukudziwa kuti mawa ndifa?” Iye anati, “Chichotse chimenecho kuno, ukungondisereula ine.” Ndipo iye sanalandire izo. Iye anati, “Ayi, ine—ine sindikufuna zimenezo.” Anati, “Iwe ukungopanga. . .” Anati, “Ngati uyo akanakhala—Purezidenti,” anati, “ilo likanakhala ndi—chidindo cha boma, ndipo ilo likanakhala ndi pepala lake loyenera.”

Iye anati, “Koma ndi siginecha yake!”

<sup>94</sup> Iye anati, “Ine ndingadziwe bwanji siginecha yake?” Iye anati, “Iwe ukungondisereula ine, ukuyesera kuti ine ndimverere bwino.” Ndipo iye anangoyamba kukuwa, natembenuza nsana wake. Mnyamatayo anawomberedwa mmawa wotsatira.

<sup>95</sup> Kenako mnyamatayo atafa, ndipo dzina la Purezidenti liri pa chidutswa cha pepala ili, kuti iye anakhululukidwa, ndiye chiyani? Ndipo iwo anakazenga izo mu bwalo lamilandu. Ndipo apa panali chigamulo cha mabwalo amilandu athu, limene liri chimake cha mabwalo amilandu athu onse. Zimene amanena nthawi zina, ife sitikonda chiganizo chawo, koma ife timayenera kutsatira izo mulimonse, mwaona, chifukwa ndicho chikhomo. Ndiwo mtheradi. Tsopano, ilo linanena lingaliro ili, “Chikhululukiro sichimakhala chikhululukiro pokhapokha ngati chitalandiridwa ngati chikhululukiro.”

<sup>96</sup> Ndipo umo ndi momwe Mawu a Mulungu amakhalira. Iwo amakhala chikhululukiro ngati Iwo alandiridwa ngati chikhululukiro. Ndipo Iwo ndi Mawu a Mulungu, Iwo ndi

mphamvu ya Mulungu, kwa iwo amene ati adzawakhulupirire Iwo ndi kuwalandira Iwo.

<sup>97</sup> Ziribe kanthu, iwe ukuyang'ana pa Iwo, ndipo nkuti, “Oh, izo zakhala zikusokonezedwa, pakhala pali zomasulira milioni, ndi zonse izo.” Izo zikhoza kukhala chomwecho kwa winawake.

<sup>98</sup> Koma, kwa ine, Iwo akanali Mawu a Mulungu, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Iye ndi wokakamizika kukhala ndi Mawu amenewo.

<sup>99</sup> Tsopano Iye akuyenera kuti adzawuweruze mpingo, tsiku lina. Ndipo ngati Iye adzawuweruze iwo ndi mpingo wa Katolika, chimene iwo amati Iye adzatero, ndiye ndi uti wa mipingo ya Katolika umene Iye ati adzaweruzire iwo? Iwo amasiyana wina ndi mzake. Ngati Iye aweruze iwo ndi Amethodisti, inu Abaptisti mwapita. Ngati Iye adzaweruze iwo ndi Achipentekoste, nonse a inu mwapita.

<sup>100</sup> Koma Iye sadzaweruzira iwo ndi mpingo. Baibulo linati, “Iye adzaweruzira dziko lapansi ndi Yesu Khristu, ndipo Khristu ndi Mawu.” Chotero inu mukuona ife tiribe chowiringula, Ndi Mawu a Mulungu, amene Iye adzatiweruzire ife; ndipo ziribe kanthu kaya ochepa bwanji, tanthauzo la mawu amodzi kwa Awa, anatero Chivumbulutso 22:18.

<sup>101</sup> Choyamba, ndiyambira mu Genesis. Mulungu anawupatsa mtundu wa anthu Mawu Ake, kuti azidzilimbikitsira nawo okha ku imfa, tchimo, ndi chisoni, kapena tsoka lililonse. Chingwe, cha Mawu Ake. “Inu musakhudze mtengo uwu, pakuti, tsiku limene mudzadya za umenewo, tsiku limenelo inu mudzafa.” Ndipo chingwe chimangokhala chabwino pamalo ake ofooka kwambiri. Ndipo miyoyo yathu imakhala ikukokedwera ku gehena, ikugwira ku chingwe ichi; kudula chimodzi cha izo, ndizo zonse zimene mukuyenera kuchita. Eva sanaswe konse chiganizo, iye anaswa Mawu, ndi Satana. Kumeneko kunali koyambirira kwa Bukhu.

<sup>102</sup> Pakati pa Bukhu panadzabwera Yesu, ndipo anati, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu aliwonse.” Osati gawo la iwo, amodzi okha apa ndi apo, koma, “Mawu aliwonse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu.”

<sup>103</sup> Pamene Iye anafa, anaukitsidwa, ndipo anapita Kumwamba, ndipo anadzabwereranso ndipo anadzampatsa Yohane... chimene Iye ananena pamenepo chitatha chiukitsiro Chake. Anati, “Nanga bwanji ngati...” Anati, “Chidzachitike ndi chiyani kwa mwamuna *uyu*?”

<sup>104</sup> Yesu anati, “Kuli chiyani kwa iwe ngati adzakhale kufikira Ine nditadza?” Osadziwa kwenikweni moyo wake ukanatero, koma utumiki wake ukanapitirira. Ndipo Iye anamukweza iye mmwamba, mu mutu wa 4 wa Chivumbulutso, ndipo anamuwonetsa iye zinthu zonse zimene zinali nkudza, zimene ife tikukhalamo, ngakhale ku mutu uwu lero.

<sup>105</sup> Ndipo kenako pa mutu wa 22, mutu wotsiriza, ndime ya 18, Iye anati, “Aliyense amene ati adzachotse Mawu amodzi mu Bukhu ili, kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo, gawo lake lidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo.” Mukuona? Chotero ife timakhulupirira kuti munthu amakhala moyo ndi Mawu aliwonse a Mulungu. Ine ndimakhulupirira zimenezo ndipo ndikudziwa kuti ndi zoonā. Zochepa bwanji, ziribe kanthu. Zimangotengera mawu amodzi, kuti achite izo.

<sup>106</sup> Kuganiza za kuchepa ndi kusafunikira, powona kuti azimzanga ambiri aku Canada akhala pano. Ndikukumbukira ine ndinali ku Canada pamene Mfumu George... Amene ine ndinali nawo mwayi wopita kukamupempherera, pamene iye anachiritsidwa, ndi kusokonezeka kwa mitsempha; iye ankavutika tsiku limenelo, ku kusokonezeka kwa mitsempha, ndiponso iye anali ndi vuto la mmimba, chilonda; monga ambiri a inu aku Canada mukudziwa, ndi Achimerika, nanunso. Koma kumuwona iye akudutsa kumeneko, atakhala mu galeta imeneyo, iye—iye anali mfumu. Iye ankachita zinthu ngati mfumu. Mfumukazi yake yokongola itakhala pafupi ndi iye, mu diresi lake la buluu, ndipo pamene iye ankabwera akutsika mmisewu.

<sup>107</sup> Ndipo mzanga wa ine, ndi ine, tinali titayima limodzi. Ndipo pamene galeta lija linkadutsa, iye anangotembenuza mutu wake ndikuyamba kulira. Ndinaika dzanja langa pa phewa lake, ndipo ndinati, “Vuto ndi chiyani?”

<sup>108</sup> Iye anati, “M’bale Branham, apo akupita mfumu yanga ndi mfumukazi yake.” Chabwino, ine—ine ndikhoza kuyamikira zimenezo.

<sup>109</sup> Ndiye ndinaganiza, “Ngati waku Canada, pansi pa wamkulu wa boma, osati wamkulu wa boma, koma komabe wamkulu wa boma, waku England, ndipo mfumuyo ikudutsa, zikukhoza kumupangitsa munthu wa ku Canada kulira, ndi kutembenuza mutu wake ndi kumalira, zidzakhala zotani tikadzawona Mfumu yathu?” Ndipo kuganiza za izo, gawo lathu lidzakhala Mfumukazi.

<sup>110</sup> Ndiye ana onse anatulutsidwa ku sukulu, ana aang’ono, iwo anapatsidwa yaying’ono, mbendera ya ku Britain. Mbendera ya Canada imatchedwa chinthu china. M’bale Fred, kodi mbendera ya Canada imatchedwa chiyani? [M’bale Fred Sothmann akuti, “Union Jack.”—Mkonzi.] Union Jack. Koma iwo anawapatsa iwo yaying’ono, mbendera ya ku Britain, kuti azigwedeza. Ndipo pamene mfumu inkadutsa, ana aang’ono onse anaimirira pamenepo, akugwedeza yawo—mbendera yawo yaying’ono, ndi kumafuulira kwa mfumuyo. Ndipo—ndipo apo panali magulu akuimba, *Mulungu Ipulumutseni Mfumu*, pamene iye ankaaguba akudutsa mumsewu.

111 Oh, ngati mutangopeza a . . . Mukanangokhala ndi kuwona mmene ziti zidzakhalire pa chiwukitsiro kumeneko!

112 Ndipo pamene iwo analangizidwa, ana aang'onowo, kuti abwerere ku sukulu mwamsanga pamene—kuguba kutatha. Ndipo, ana aang'onowo akubwerera, sukulu ina inasowa mtsikana wamng'ono. Ndipo iwo anapita kulikonse, kuti akamupeze munthu wamng'onoyo, chokwera ndi chotsika mmisewu. Ndipo, potsiriza, kuseri kwa polo la foni, kunayima mtsikana wamng'onoyo, wochepa, wamng'ono, wamfupi, akungolira mtima wake mofuula.

113 Chabwino, mphunzitsi anamunyamula iye ndipo . . . [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. “Vuto ndi chiyani? Kodi sunamuwone mfumu?”

Iye anati, “Inde, ndinaiwona mfumuyo.”

Anati, “Kodi—kodi iwe sunagwedeze mbendera yako?”

Iye anati, “Inde, ine—ndinagwedeza mbendera yanga.”

Iye anati, “Chabwino, ndiye, iwe nchifukwa chiyani ukulira?”

114 Iye anati, “Inu mwaona, aphunzitsi, ndine wamng'ono kwambiri, enawo anayima kutsogolo kwanga, anali aakulu. Ndipo ndinagwedeza mbendera yanga, koma iye sanaiwone iyo.” Ndipo iye anasokonezeka nazo zimenezo. Chabwino, izo zikhoza kukhala kuti Mfumu George sanamuwone munthu wamng'onoyo, mu usinkhu. Iye mwina sanawone mtima wake wokonda dziko, ndi momwe iye ankamverera za iye. Iye anali wamfupi kwambiri.

115 Koma izo si chomwecho ndi Mfumu yathu! Oh, kanthu kakang'ono kwambiri kamene ife timachita, Iye amakawona iko. Ndipo Iye amadziwa zinthu ndi malingaliro amene ali mmitima yathu, chirichonse chimene ife timachita, chaching'ono chimene icho chiri. Ndipo kodi ife timamutumikira motani Iye? Pamene titumikirana wina ndi mzake. Ngati sindikukondani inu, ndingamukonde bwanji Iye? Mukuona? “Mochuluka monga inu mwachitira kwa aang'ono Anga awa, inu mwandichitira Ine.” Mukuona?

116 Ndi—ndi zinthu zazing'ono zimene timazisiya osazichita, nthawizina, zimene zimadula chingwe chonsecho, inu mwaona, ndipo tiyeni timasuke, basi amalingaliro achipembedzo, ndipo tiwale za zinthu zazing'ono izi zimene ziri kwenikweni—zinthu zofunikira. Chirichonse, Mawu aliwonse a Mulungu, ndi ofunikira. Palibe aliwonse a Iwo amene angasiyidwe. Ife tikuyenera kutenga Mawu aliwonse a Iwo, basi momwe Iwo analembedwera.

117 “Ndayima pakhomo,” anatero Yesu, mu M'badwo wa Laodikaya uwu, “ndipo ndikugogoda.” Kodi inu munazindikira, m'badwo wa mpingo wokhawo umene Iye anachotsedwa mu

Mpingo Wake? Mibadwo ina yonse ya mpingo, Iye anali mkati mwa mpingo. Kudutsa Methodisti, ndi Achilutera, ndi ena otero, Iye anali mkati, mpingo. Koma apa Iye ali kunja, tizikhulupiriro tathu ndi zinthu zinali zitamuthamangitsa Iye mu mpingo. Koma Iye wayima kunja uko, akugogodabe, “Iye amene adzamva ndi kutsegula chitseko, ndidzalowa ndi iye, nkudya nawo iwo, ndi kumupatsa iye machiritso ku maso ake, ndi—ndi zovala, ndi kumupatsa iye chuma cha Kumwamba; iye amene adzandimva Ine ndikugogoda.”

<sup>118</sup> Ndimaganiza kuti nditha kuganiza za dzina la wojambula amene anajambula chithunzi chimenecho, anapenta chithunzicho, kani, cha pakhomo. Pamene iye... Inu mukudziwa, zithunzi zonse zazikulu zikuyenera kudutsa pamzere, kapena, holo ya otsutsa, icho chisanapachikidwe mu Holo ya Otchuka. Chojambula chapachiyambicho tsopano chingagulitsidwe mamillions a madolla.

<sup>119</sup> Koma, mwaona, ziri ngati Mpingo, ukuyenera kudutsa mu holo ya otsutsa. Ife timadutsamo. Inu mudzatchedwa “woyera-wodzigidubuza,” inu muzidzatchedwa chirichonse. Koma ngati inu mungakhoze kungogwira malo anu mwa Khristu, ndiye tsiku lina Iye adzatitengera ife ku Holo ya Otchuka. Koma choyamba tikuyenera kupirira kutsutsidwa. Apo ndi pamene kuchepa kwathu kwayima, apo ndi pamene izo zimawonetsera. “Iye amene sangathe kupirira chilango ndi mwana wapathengo, ndipo osati mwana wa Mulungu.” Ziribe kanthu momwe iye wajowinira mpingo, ndi chirichonse chimene iye wachita, iye akanali, ngati iye sangathe kupirira chilango, iye ndi wapathengo, ndipo iye si mwana weniweni wa Mulungu. Koma weniweni, mwana weniweni wa Mulungu samasamala chimene dziko likunena, china chirichonse ndi chachiwiri. Iye wayika malingaliro ake pa Khristu, ndipo izo zimakhazikitsa izo. Inde. Chirichonse chimene Khristu anena kuti achite, iye adzachichita. Kulikonse kumene Mwanawankhosa akupita, iwo ali ndi Iye, kulikonseko. Ndiyeno mudzawona kuwonekera Kwake, Kukhalapo Kwake, ndi chimene Iye akuchita. Iye nthawizonse amakhala ndi anthu Ake, Mkwatibwi Wake. Iye ali pa ubwenzi ndi iye. Tsiku lina kudzakhala Mgonero wa Ukwati.

<sup>120</sup> Ndipo wojambula uyu, komabe, pamene icho chinadutsa mwa otsutsa, gulu la otsutsa linasonkhana mozungulira wojambula uyu. Sindingathe kuganiza dzina lake. Ine ndikuyesera kuganizira za Michelangelo, koma iye anali wosema wa chipilala cha Mose. Koma ndikulephera kuganiza dzina lake. Koma, komabe, iye anati, “Chithunzi chako ndi chapamwamba,” anati, “Ndiribe chimene ndinganene motsutsana ndi chithunzicho.” Iye anati, “Chifukwa, Iye wanyamula nyali m’dzanja Lake, izo zikusonyeza kuti Iye amabwera, nayenso, mu usiku wa mdima waukulu.” Iye anati, “Ndiyeno Iye ali pakhomo, ndi mutu Wake, khutu Lake,

kuchitira kuti Iye asati. . . kufuna kutsimikiza kuti asaphonye kuyitana kotsikitsitsako. Iye watembenezira khutu Lake kuchitseko, ndipo Iye akumenya chitseko.” Iye anati, “Koma, inu mukudziwa, bwana, pali chinthu chimodzi chimene inu munayiwala pa chithunzi chanucho.”

<sup>121</sup> Ndipo wojambulayo, zitamutengera iye moyo wake wonse kuti ajambule icho, iye anati, “Ndi chiyani chimene ine ndayiwala, bwana?”

<sup>122</sup> Iye anati, “Ziribe kanthu kuti Iye wagogoda mochuluka bwanji, mwaona, inu munaiwala kuika chotsekera pa icho. Palibepo chotsekera pa chitsekocho.” Ngati mungawone chitsekocho, palibepo chotsekera.

<sup>123</sup> “Oh,” anatero wojambulayo, “Ndinajambula icho chomwecho. Mwaona, bwana,” iye anati, “chotsekera chiri mkati. Inu ndi amene mumatsegula chitsekocho. Inu mumatsegula chitseko.”

<sup>124</sup> Oh, kodi munthu amagogoderanji pa chitseko cha munthu? Iye amakhala akuyesetsa kuti alowe. Iye akuyesetsa kuti alowe mkati. Mwinamwake ali ndi chinachake akufuna kukuuzani kapena kukambirana nanu. Iye ali ndi uthenga wa kwa inu. Ndipo ndicho chifukwa chimene anthu amagogodera pa khomo la wina ndi mzake. Iwo amakhala ndi chifukwa china chochitira izo. Sipangakhale izo zikuchitika popanda chifukwa china. Simungapite ku nyumba ya munthu pokhapokha ngati pali chifukwa china chopitira; ngati palibe chirichonse, chokamuyendera, kumutengera uthenga, kapena chinachake. Pamakhala chifukwa china choti munthu apite kukagogoda pakhomo la munthu wina.

<sup>125</sup> Paliponse pamene pali funso, pamayenera kukhala yankho. Sipangakhale funso popanda yankho. Chotero ndi chimene ife timachiyang’ana mu Baibulo, mafunso awa a lero, Baibulo liri nalo yankho. Ndipo Khristu ndi Yankho limenelo.

<sup>126</sup> Tsopano, anthu ambiri ofunikira agogodapo pazitseko, kudutsa nthawi ya moyo, ndipo ambiri agogodapo mu nthawi zakale; ndipo pamenepo mwinamwake, nthawi zikupitirira, padzakhala ochuluka, anthu ofunikira.

<sup>127</sup> Tsopano, chinthu choyambirira, mwinamwake, ngati winawake akugogoda pakhomo panu, ngati inu mungathe, inu mungazembere ndi kudzakokera katani mmbuyo, kudzawona yemwe ali pamenepoyo.

<sup>128</sup> Ngati muli otanganidwa, monga timanenera kuti tiri lero, “Wotanganidwa kwambiri kuti upite ku tchalitchi; otanganidwa kwambiri kuchita *ichi*. Ndipo, inu mukudziwa, mpingo wanga sumakhulupirira mu zinthu za mtundu umenewo.” Ndipo, mwaona, ife timakhala kuti tachoka pa njira, nthawizina, kuchoka ku Mawu.

129 Koma inu mumakokera katani mmbuyo, ndiye inu mumafuna kuti muwone amene wayima pamenepoyo. Ndipo ngati ali munthu wofunikira, mwamsanga mumathamangira pa chitseko.

130 Tsopano tiyeni tibwerere mmbuyo pang'ono pokha, ndipo titenge anthu ochepa amene anagogodapo. Tiyeni tibwerere mmbuyo ndi kulingalira za Farao mu Igupto, zaka mahandiredede zambiri zapitazo. Nanga bwanji—ngati Farao, mfumu ya Igupto, akanatsikira ku nyumba ya munthu wamba? Ndipo munthu wamba uyu anakhala ngati wosagwirizana ndi Farao, ndipo iye sankakhulupirira ndondomeko zake, ndipo anasiyana naye iye. Ndipo—ndipo, koma apa payima Farao, ataimirira pakhomo la—womanga nyumba kapena wothona matope, monga ife tingawatchulire iwo, uko mu Igupto. Ndipo iye akukokera katani yake mmbuyo, ndipo apo payima Farao wamphamvu pa chitseko. Ndipo akugogoda; akumwetulira pankhope pake. [M'bale Branham akugogoda pa chinachake—Mkonzi]. Bwanji, munthu wa wamba ameneyo akhoza kutsegula chitseko, ndikuti, “Lowani, Farao wamkulu, mulole wantchito wanu wodzichepetsa apezese chisomo pamaso panu. Ngati pali kalikonse mkati mwa makoma anga, ine ndiri ngati kapolo kwa inu, Farao. Mwandilemekeza ine kuposa abale anga. Inu mwabwera kunyumba kwanga, pamene ine ndiri munthu wosauka. Inu mumangoyendera mafumu ndi—ndi olemekazeka, ndi anthu ofunika. Ndipo ine ndi wosafunikira. Koma inu—inu mwandiyendera ine, inu mwandilemekeza ine, Farao. Kodi wantchito wanu wodzichepetsa achite chiyani?” Ziribe kanthu chimene Farao akanapempha, ngakhale pa moyo wake, iye akanawupereka iwo. Ndithudi. Ndi ulemu.

131 Kapena, tinene mwachitsanzo, malemu Adolf Hitler, pamene anali Mtsogoleri wankhanza waku Germany. Bwanji ngati iye akanapita ku nyumba ya msirikali? Ndipo gulu lija la asirikali aang'ono a Nazi onse atamanga misasa mozungulira, ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, bwanji, winawake kugogoda pa chitseko. Ndipo msirikali wamng'onoyo nkuti, “Ah, ndikumverera moipa mmawa uno! Mkazanga, awuze iwo kuti azipita.”

132 Ndipo iye anazembera ku chitseko, ndipo nakokera kataniyo mmbuyo. Iye nati, “Mwamunanga! Mwamunanga, lumpaha mmwamba, mwamsanga!”

“Vuto ndi chiyani? Ndani wayima pamenepo?”

“Hitler, Mtsogoleri woopsya waku Germany!” Oh, mai!

133 Msilikari wamng'onoyo kulumphira panja, kuvala zovala zake, mwamsanga, ndipo nkudzayima njoo. Nkudzayenda kupita apo pa chitseko, nkudzatsegula chitsekocho, ndipo nkutsegula chitsekocho, ndi kudzati, “Tikuoneni Hitler!”



Mwaona, iye anali munthu wamkulu, masiku ake mu Germany. “Kodi ine ndichite chiyani?”

<sup>134</sup> Ngati iye akanati, “Pita ukalumphe pa phompho kunja uko,” iye akanachita izo. Chifukwa? Palibenso, palibenso munthu wofunika kwambiri mu Germany, mmasiku a Nazi, kuposa Adolf Hitler. Iye anali munthu wamkulu. Ndipo iye. . . Ndipo, ndi ulemu bwanji, pamene iye amangochezera akulu ankondo okha ndi amuna aakulu, koma apa iye ali pakhomo la woyenda pansu! Oh, ndithudi ukanakhala ulemu waukulu kwa iye.

<sup>135</sup> Chabwino, tsopano, nanga bwanji Flagstaff? Tizibweretse pafupi ndi kwathu. Nanga bwanji madzulo ano, kuti—kuti Purezidenti wathu, Bambo Johnson, L. B. Johnson, nanga bwanji ngati iye akanatsika mu ndege, kunja kuno kwinkwaka? Ndipo tsopano ife tonse tiri mu gulu limodzi la anthu. Ndife tonse osauka. Mwinamwake wina ali ndi ntchito yabwinoko pang’ono, mwinamwake nyumba yabwinoko pang’ono, koma, pambuyo pa zonse, ndife anthu chabe. Koma bwanji ngati iye atabwera kunyumba kwanu kumusi kuno, mwinamwake wodzichepetsa kwambiri wa ife, ndipo iye nkudzagogoda pa chitseko; ndipo inu nkudzapita pa chitseko, ndipo apo payima Purezidenti L. B. Johnson? Bwanji, iwo ungakhale ulemu waukulu. Inu mukhoza kusiyana ndi iye, mu ndale. Koma inu mungakhale munthu wolemekezeka, kukhala ndi Purezidenti wa United States ataima pakhomo panu. Inu ndi ndani kapena ine ndi ndani? Ndipo apo payima Lyndon Johnson pakhomo panu! Ngakhale mukhoza kukhala wa Socialist kapena Republican, kapena kusiyana naye mailosi milioni, komabe ukhoza kukhala ulemu.

<sup>136</sup> Inu mukudziwa chiyani? Chifukwa choti inu munapatsidwa ulemu uwu, bwanji, televizioni ingakaziyeke izo pa sikilini usikuuno. Ndithudi. Manyuzipepala apakati mawa akanakhala ndi mitu yankhani mmenemo, muno mu pepala la Flagstaff, kuti, “*John Doe*. Purezidenti waku United States anawulukira ku Flagstaff dzulo, wosaitanidwa, ndipo anangopita kumeneko, popanda ngakhale kuyitanidwa, ndipo anakagogoda” pachitseko chanu. Wodzichepetsa! Purezidenti ameneyo angakhale ndi dzina la kukhala munthu wodzichepetsa, wamkulu mmene iye aliri, kuti angabwere kwa changa kapena chitseko chanu; ife sitiri kanthu, kenako anabwera ndi kudzayankhula nafe ife.

<sup>137</sup> Bwanji, inu mungayende mu msewu, ndikuti, “Inde, ndine munthuyo. Purezidenti anadzandichezera ine.”

<sup>138</sup> “Imani njii, ndiloleni nditenge chanu—nditenge chithunzi chanu. Tayang’anani molunjika pa ine. Tsopano mukuoneka bwanji mukachokapo?” Inu mungakhale munthu wofunikira. Ndithudi.

139 Nanga bwanji ngati mfumukazi ya ku England itabwera, ngakhale simuli pansi pa ulamuliro wake? Koma chingakhale chaulemu kwa ena a akazi inu kukaisangalatsa mfumukazi ya ku England, ngakhale simuli pansi pa ulamuliro wake. Koma, komabe iye ndi munthu wamkulu, iye ndi mfumukazi yaikulu kwambiri mu dziko, pa nthawi ino. Ndithudi, iye ali, ndiko kuyankhula mwa ndale. Koma ngati iye atakupemphani ngale ina yaying'ono pakhoma panu, imene ndi yamtengo wapatali kwa inu, inu mungaipereke iyo kwa iye. Zingakhale zaulemu kwa inu kuchita zimenezo. Ndithudi, iyeyo ndi mfumukazi ya ku England.

140 Ndipo inu mungalemekezede, ndi Purezidenti. Ndipo aliyense angayankhule za kudzichepetsa kwa mfumukazi ya ku England, kuwulukira uko kuti akamuwone mkazi winawake mu Flagstaff, wosadziwika wamng'ono. Ndipo mapepala angakhoze kulemba zimenezo, ndipo nkhani zingalengeze izo.

141 Koma, inu mukudziwa, Munthu wofunikira kwambiri wa nthawi zonse, Yesu Khristu, amagogoda pakhomo lathu. Ndipo Iye amakanizidwa, kuposa mafumu onse ndi amphamvu amene anayamba akhalapo. Uko nkulondola. Ndipo inu mukhoza kumulandira Iye ndi kupita kumeneko ndi kukanena chinachake cha izo, dziko lakunja lingakusekeni pa nkhope yanu. Palibe nkhani yonenedwapo. . .

142 Ndani angabwere kunyumba kwanu, wamkulu woposa Yesu Khristu? Ndani angagogode pakhomo panu, wamkulu kuposa Yesu Khristu? Ndani angachite zimenezo? Mwana wa Mulungu, amene angagogode pa nyumba yanu, ndani angakhale wofunikira kwambiri? Ndipo komabe Iye amagogoda, tsiku ndi tsiku. Ndipo ngati inu mumulandira nkomwe Iye, inu mumatchedwa wotengeka. Chotero, mukuona momwe dziko limadziwira ake omwe? Uko nkulondola. Koma tsopano Iye sangabwere pokhapokha ngati Iye atakhala ndi chifukwa choti abwerere.

143 Ndipo kodi inu mukuganiza kudzichepetsa kwa Purezidenti Johnson, kapena mfumukazi ya ku England, kapena munthu wamkulu aliyense, mmene zikanawonetsedwera, za kudzichepetsa kwa munthu wofunika kwambiri ameneyo akugogoda pa chitseko chanu!

144 Nanga bwanji za kudzichepetsa kwa Mwana wa Mulungu? Ndife ndani koma ochimwa, odetsedwa, “obadwa mu tchimo, owumbidwa mu kusaeruzika, obwera mdziko tikuyankhula mabodza?” Ndipo kenako Mwana wa Mulungu nkubwera ndi kudzagogoda pa chitseko chathu.

145 Tsopano, mfumukazi yaku England ikhoza kukupemphani chinthu. Iye akhoza kutenga chinachake kwa inu. Chomwechonso Purezidenti, akhoza kukufunsani inu kuti muchite zinthu zimene inu simumafuna kuchita. Iye akhoza

kukufunsani inu chuma chimene inu simunafune kuchipereka, ndipo chimene sichingatanthauze kanthu, chabe kwa iye.

<sup>146</sup> Koma Yesu akubweretsa chinachake kwa inu pamene Iye akugogoda. Iye akubweretsa chikhululukiro. Musachikane icho. Pakuti, monga izo zinazengedwa mu makhothi athu kuno, chomwechonso izo zidzakhala mu Ufumu wa Kumwamba. Ngati Iye anagogoda ndi kubweretsa chikhululukiro, ndipo inu munachikana icho, ndi kufa mu machimo anu, inu mudzawonongeka; ngakhale munali ndi mwayi wokhala pa msonkhano wonga uwu, ngakhale munali ndi mwayi wokhala pa chitsitsimutso, kapena mpingo wanu, ndipo kumva abusa anu akulalikira uthenga wa Uthenga. Ndipo munali ndi omvetsera, ndikuti, “Inde, ndinali kumeneko.” Mwinamwake, inu, zovuta kunena chimene inu nonse mukananena. “Ndinamva kuyimba. Ndinasangalala nazo. Ndinamva maumboni. Zinali zenizeni.” Koma inu munakana Iwo.

<sup>147</sup> Bwanji ngati ine ndikanakhala mnyamata wamng’ono ndikumpeza dona wamng’ono; iye anali wokongola, iye anali Mkhristu? Iye akanapanga...Iye anali aliyense woyene... [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Inu simungapeze cholakwika ndi Iwo, koma inu mukuyenera kuika pambali miyambo ya anthu. Inu mukuti, “Oh, ine ndikukhulupirira Uko ndi kulondola. Ine ndikuwona, ndakhazikika...” Koma inu mukuyenera kuwalandira Iwo. Inu...Ndiye mkazi ameneyo amakhala gawo la ine. Ndiye inu mumakhala gawo la Mawu, amene ali Mkwatibwi. Ngati Iye ali Mawu, Mkwatibwi adzakhala Mkwatibwi wa Mawu. Mwaona, ndithudi adzatero! Mwaona, inu mukuyenera kuwalandira Iwo. Inu mungatero... Inu mukhoza kunena chimene mukufuna, inu mukhoza kubwekerera za Purezidenti; koma kawirikawiri pamene nthawi ya Yesu ifika pakhomo pathu, ife timangomukankhira Iye kumbali. Mwaona, basi ife sitimafuna kanthu kochita ndi Iye. Ife timati, “Chabwino, tsiku lina.”

<sup>148</sup> Bwanji ngati mutagogoda pakhomo la munthu? Tsopano tiyeni tingotembenuza chithunzicho kwa mphindi imodzi. Bwanji ngati inu mutapita ndi kukagogoda pa chitseko cha winawake, ndipo inu munali ndi chinachake cha iwo? Ndipo, kuwonjezera apo, iwo anali kwa inu monga inu mungakhalire kwa Mulungu; chabwino, ngati inu mutero, bwanji, chabwino, koma inu mulibe zingwe zomangidwa nazo. Chotero pamene inu munagogoda pa chitseko cha winawake, ndipo iwo anasuzumira pa zenera, ndi kutseka katani; kapena anabwera pa chitseko, ndi kudzati, “Nthawi ina!”

“Chabwino, ine ndikufuna...”

<sup>149</sup> “Ine ndiribe nthawi mmawa uno!” Kodi mukudziwa chimene mungachite? Mwinamwake chinthu chomwecho

chimene ine ndikanachita, ndi ena onse a iwo, inu simungabwererekonso.

<sup>150</sup> Koma osati Yesu. “Ndayima, ndipo ndikugogoda,” kugogoda mosalekeza. [M’bale Branham akupitiriza kugogoda pa chinachake—Mkonzi]. Mukuona? “Iye amene amafunafuna,” osati kufuna. “Amafunafuna! Iye amene amagogoda!” Kugogoda, kugogoda ndi kupitirira, amagogoda! Mwaona, “Iye amene afunafuna, iye amene amagogoda, chidza . . .” Osati basi . . .

<sup>151</sup> Monga fanizo la woweruza wosalungama. Mkaziyo anapita ndipo ankafuna kubwezera, kubwezera, koma sanathe kupeza izo. Iye . . . Mosalekeza amagogoda ndi kuchonderera. Ndipo anati . . . “Kungoti athane naye iye, ndidzambwezera mdani wake.”

<sup>152</sup> Ndi mochuluka bwanji adzachitire Atate a Kumwamba? Mwaona, izo zikuyenera kukhala ife tikugogoda pa khomo Lake. Zimayenera kukhala Adamu akuthamanga chokwera ndi chotsika mmundamo, akufuula, “Atate! Atate, kodi Inu muli kuti?” Koma mmalo mwake, mmalo mwa zimenezo, anali Mulungu akuthamanga chokwera ndi chotsika mmundamo, “Mwana! Mwana, uli kuti?” Mwaona, izo zimangowonetsera chimene ife tiri. Ife nthawizonse timabisala, mmalo motulukira ndi kumadzavomereza izo. Ife timayesera kuthamanga, kudzabisala kuseri kwa chinachake. Limenero ndiro khalidwe basi la munthu, ife timakhala nazo izo mwanjira imeneyo. Inde, bwana.

<sup>153</sup> Inu mukanawapatsa anthu awa zabwino kwambiri zimene inu munali nazo, chirichonse. Koma inu simungatero, inu—inu—simungamulandire Yesu. Ine sindikutanthauza inu, koma ine ndikutanthauza anthu apa.

<sup>154</sup> Kapena mwinamwake inu mukhoza kunena ichi, mukhoza kunena kuti, “Mlaliki, ine ndangochita kumene zimenezo. Ine—ine ndinangotsegula mtima wanga ndi kumulola Yesu kuti alowe. Ine ndinachita zimenezo zaka teni zapitazo. Ine ndinachita zimenezo zaka twente zapitazo.” Chabwino, izo zikhoza kukhala zolondola ndendende, koma kodi ndizo zonse zimene mwachita? Mukuona?

<sup>155</sup> Ine ndikufuna ndikufunsemi inu tsopano. Ngati mungamuitane aliyense mnyumba mwanu, ndipo kenako pamene mulowa mkati pakhomo . . . Wina wakuitanirani inu mkati, kani, ndikuti, “Lowani.”

<sup>156</sup> “Inde, ine ndiri ndi cholinga, ine ndipita kunja kwa mzinda ndi kukapatsidwa ulemu, inu mwaona.” Umo ndi momwe anthu ambiri amamulandirira Khristu. “Ine ndidza . . . Ine—ine ndi wa mpingo. Ine ndi wa ku malo aakulu *Akuti-ndi-akuti* kumusi kuno, kumene Dokotala Ph. LL. amapitako, inu mukudziwa. Ndipo iwo ndi mpingo waukulu kwambiri. Ameya amapita

kumeneke, ndi chirichonse, inu mukudziwa. Ine—ine ndi wa mpingo umenewo.” Iwo amamulola Iye kulowa, mochuluka chomwecho. “Eya, ndidzambulandira Iye,” mwaona, kuti apeze phindu la iwoeni.

157 Koma nanga bwanji pamene Yesu abwera mu mtima? Anthu ambiri amamuvomereza Iye chifukwa iwo sakufuna kupita ku gehena. Koma pamene Yesu abwera mu mtima mwanu, Iye amafuna adzakhale Ambuye. Osati Mpulumutsi chabe; koma Ambuye, nayenso. *Ambuye* ndi “ulamuliro.” Iye amabweramo ku—kudzatenga ulamuliro.

Tsopano inu mukuti, “Nkulondola kumeneke, M’bale Branham?” Ndithudi.

158 Nanga bwanji ngati—ngati nditakuitanani inu kunyumba kwanga, ndipo inu nkudzalowa pakhomo? Ndipo inu munadzagogoda pakhomo, ndipo ine nkudzayang’ana panja, ine nkuti, “Inde, lowani mkati. Ngati mungathe kundithandiza ine, chabwino, inu mutero. Koma tsopano, mukalowa mkati muno tsopano, sindikufuna kuti muzisokoneza mnyumba mwanga. Inu mungoima pomwepo pa chitseko!”

159 Kumbukirani, mutu wathu ndi “zitseko” mkati mwa chitseko. Tsopano, mkati mwa mtima wa munthu muli zitseko zazing’ono zambiri, ndipo zitseko zazing’ono zimaphimba zinthu zambiri. Kungomulola Iye kuti alowe, izo si zonse za izo, pamene Iye alowa mkati.

160 Pamene ine ndilowa mnyumba mwanu, ngati inu mwandilandira ine pa chitseko, bwanji, ngati inu mungati, “Lowani mkati, M’bale Branham. Ndine wokondwa kukuonani inu!”

161 Ine ndingati, “Chabwino, ndi chamwayi kwa ine kulowa mnyumba mwanu!”

162 “Oh, kodi inu simubwera ndi kudzakhala pansu? M’bale Branham, dutsani mnyumba mwathu, mudzipange nokha kuti muli kwanu!” Oh, mai!

163 Ndingapite ku firiji, kukadzitengera imodzi ya masangweji aakulu awo, monga *choncho*, kuvula nsapato zanga, ndi kupita ku chipinda ndi kukagona pansu. Ndipo ine ndingakhale ndi—phwando lenileni la chisangalalo, mwaona. Bwanji? Chifukwa ndamverera kuti ndalandiridwa bwino. Inu mwandilandira bwino. Chifukwa chake ndingayamikire ngati mwandipanga ine wolandiridwa bwino.

164 Koma ngati nditalowa mnyumba mwanu, ndipo inu nkundiuzwa ine, “Inu muyime pamenepo pakhomo, tsopano, musayambe kuyendayenda!” Ine sindingamverere kuti ndalandiridwa kwambiri. Inu mungatero? Ayi, mwaona, simungamverere kuti mwalandiridwa. Winawake atakuitanani

inu, ndipo nkuti, “Tsopano dikirani! Eya, dzaloweni, koma muyime pamene!”

<sup>165</sup> Tsopano, pali chitseko chaching’ono pamene inu mubwera mu mtima wa munthu. Ife tingoyankhula za zingapo za izo, mwaona. Ife tiribe nthawi kuti tidutse mu zitseko zonsezi, chifukwa ziripo zochuluka za izo. Mukuona? Koma, titi, maminiti teni otsatira, tiyeni tiyankhule za zingapo, zitseko zitatu.

<sup>166</sup> Tsopano, ku dzanja lamanja la mtima wa munthu, pamene inu mulowa pa chitsekocho, pali chitseko chaching’ono kumbali ya kumanja, ndipo icho chimatchedwa, mmenemo, chitseko cha kunyada. Oh, mai! “Inu musapite kukalowa pa chitseko chimenecho!” Iwo sakuwafuna Ambuye mmenemo, pa khomo limenelo, ndiko kunyada. “Ndine wa magazi abuluu. Ine ndimasamala! Oh, inde, tsopano taonani, ndikuuzani, ine—ine...” Mwaona, ndi kunyada. “Inu musakasokoneze mmenemo!” Tsopano, Iye sangamverere kulandiridwa ngati inu mutatseka chitseko cha kunyada chimenecho.

<sup>167</sup> Iye akuyenera kukuchititsani manyazi. Mwaona, ndicho chimene Iye amabwerera. “Inu mukutanthauza kundiuza kuti ndikuyenera kupita kumusi kumeneko—ndi kukachita monga ena onse?” Chabwino, simukuyenera kukatero, ndicho chinthu chimodzi chotsimikizika. “Chabwino, ndikuuzani inu, mukuganiza kuti ndingakachite chiyani nditapita ku bungwe la zamalonda nthawi yotsatira? Ndingakachite chiyani nditakakumana ndi wanga—bwana wanga mawa? Ndipo kuti, ine ndiyenera kukawuyika Mzimu umenewo pa ine, ndipo nkukalumphira pamwamba apo, pakati pa ntchito yanga, ndipo nkuyamba kuyankhula mmalirime, oh, izo zingandichititse manyazi ine. Ayi, kakhaleni kunja pamene!”

<sup>168</sup> Mwaona, ndi inu pamene, mwaona. Eya, inu mumulola Yesu kulowa mkati, inu mudzajowina mpingo ndi kukaikapo dzina lanu, kumalandira Yesu ngati Mpulumutsi wanu; koma nanga bwanji kukhala Ambuye wanu, pamene Iye amakhala ndi ulamuliro wonse? Pamene Iye akhala Ambuye, Iye amalambulira zonse, ndipo mumakhala wa Iyeyo; inu, inu mumadzipereka kwathunthu kwa Iye tsopano.

<sup>169</sup> Koma kunyada pang’ono kumeneko. “Oh, inu mukutanthauza, kwa ife akazi, ife tizilola tsitsi lathu kuti likule?” Chabwino, icho ndi chimene Iye ananena. “Ife tisiya kuyika zonyezimiritsa, kapena zinthu zodzipaka?” Ndicho chimene Iye ananena. “Chabwino, mukuganiza kuti bwalo langa losoka lingatani? Iwo adzanditcha ine wakachitidwekachikale.” Chabwino, ingosungani kunyada kwanu. Zipitani chitsogolo. Iye adzayima pa chitseko, ndizo zonse zimene Iye angathe kuzifikira.

170 Koma pamene inu mwakonzeka kuti mutsegule chitseko chimenecho, kumulola Iye kuti alowe, Iye adzakuyeretserani inu zimenezo. Akabudula adzapita muno mu chitini cha zinyalala, ndipo zodzipakapaka zidzabwereranso ku chitini cha zinyalala, ndipo wometa tsitsi adzafa ndi njala ngati iye amangometa tsitsi la akazi, kwa wokhulupirira weniweni.

171 Tsopano mukuti, “Izo sizitero!” Oh, inde, izo zimatero, nazonso. Ndicho chimene Baibulo linanena. Uko nkulondola. Mwaona, pali mawu aang’ono pamene, amene inu simukufuna kuti Iye asokoneze.

“Chabwino, abusa anga!”

172 Sindikusamala chimene abusa ananena. Ndi chimene Baibulo linanena, “Ndi chamanyazi kwa mkazi kutero.”

173 “Chabwino,” inu mukuti, “ife muyenera kutiphunzitsa ife zinthu, M’bale Branham, ndi momwe tingalandirire Mzimu Woyera, ndi momwe tingakhalire *ichi, icho*.” Muphunzira bwanji algebra ngati simukudziwa ma ABC anu? Simukudziwa ngakhale momwe, mungachitire ngati, kuwoneka ngati mmodzi, kuvala ngati mmodzi. Ndi chamanyazi kuwona akazi awa ali mu msewu lero.

174 Ine ndinapita ku malo dzulo, pamene, oh, ena a gulu la zigawenga zopotozedwa anadzalowamo. Iwo, amunawo anali ndi tsitsi mmaso mwawo, anabwera kumeneko ndipo likulendewera pansu ku nsana kwawo, ndi monga zovala zothina, monga ana aang’ono amavalira ku sukulu, atavala nsapato zazikulu kwambiri zakale, kukamwa kotsegula mwatheka. Mutha kudziwa kuti anali opanda makhalidwe. Ndipo anadzalowa mmenemo monga choncho, akuti, “Ndife achi French.”

175 Ndi ndani mdziko amene angamulembe ntchito munthu woteroyo pa bizinesi yake? Kodi amakhala moyo chotani? Ndipo ine ndinawona anyamata enieni angapo atakhala pamene. . . Iwo amachokera ku yunivesite kumusi uko, anyamata awa anatero, kapena ine ndikukhulupirira iwo amadzitcha okha *nsikidzi* kapena *tizirombo*, kapena chinachake chonga izo, zina za zinthu izo zikuchokera ku England. Ndipo kenako mmenemo monga choncho, ndani angamulembe ntchito munthu ngati ameneyo kuti azimugwirira iye ntchito? Kodi inu mungamuyike mwamuna ngati ameneyo mu bizinesi yanu, inu amuna azamalonda? Ngati inu mungatero, inu muli, pali chinachake, kodi inu simunafike pafupi mokwanira ku Mtanda apobe.

176 Tayang’anani pa akazi awa pa msewu, ndipo ndi chamanyazi! Mwinamwake aakazi aang’ono osalakwa atavala zovala zazing’ono izi, mwaona, chabwino, ndi chamanyazi, momwe iwo amawonekera. Chabwino, iwe nkuti, “Bwanji, mkazi, iwe ukuchita chigololo.”

<sup>177</sup> Iwo amati, “Dikira miniti apa, mnyamata! Ndine namwali basi monga ine ndiriri. . .” Izo zikhoza kukhala chomwecho, mmalingaliro akowo. Ndipo izo zikhoza kukhala chomwecho, kutsimikizira ngakhale mwa kufufuza kwa chipatala, kuti iwe ukhoza kukhala.

<sup>178</sup> Koma, kumbukirani, pa Tsiku la Chiweruzo, inu mudzakayankha chifukwa chochita chigololo. Yesu anati, “Aliyense amene ayang’ana pa mkazi nkumusirira iye wachita naye chigololo mumtima mwake,” ndipo inu munadzipereka nokha kwa iye. Mukuona momwe mdierekezi wawachititsira iwo khungu? Ndi chamanyazi. Ndi zamanyazi. Inu mwaona, iwo—iwo ali ndi mzimu. Ndi mzimu umene umachita zimenezo. Ndi mzimu wosayera.

<sup>179</sup> Koma Mzimu Woyera weniweni umamupangitsa mkazi kuvala moyenera ndi kumawoneka woyera.

<sup>180</sup> Mkazi wanga ananena kwa ine, nthawi ina. Ife tinkapita kumusi mu msewu, ndipo tinampeza mkazi atavala diresi, uko mdziko lathu. Icho chinali chinthu chachirendo kwambiri, mwaona, osati Achipentekoste ochuluka kwambiri kumbuyo uko. Chotero, ife tikupeza kuti iye anali atavala diresi. Ndipo iye anati, “Billy,” anati, “Ine ndikuwadziwa ena a akazi amenewo. Iwo amaimba mu makwaya kumusi kuno ku matchalitchi awa.”

Ine ndinati, “Ndithudi.”

Anati, “Chabwino, ndipo iwo amadzinenera kuti ndi Akhristu?”

Ine ndinati, “Wokonedwa, tayang’ana. Waona, ife sitiri. . .”

Anati, “Chifukwa chiyani anthu athu?”

Ine ndinati, “Taona, wokonedwa, sitiri a iwo—a mtundu wawo nkomwe.”

Iye anati, “Chiyani?” Anati, “Iwo ndi Achimerika.”

Ine ndinati, “Eya, koma ife sitiri.”

Iye anati, “Ife sitiri?”

Ine ndinati, “Ayi.”

<sup>181</sup> Ine ndinati, “Ndikapita ku Germany, ndimakapezako mzimu waku Germany. Pamene ndinapita ku Finland. . .” Ku sauna kumtunda uko, ambiri a inu Achifinishi mukudziwa, akazi amawasambitsa amuna. Chotero, umenewo ndi mzimu Wachifinishi basi. Anthu abwino amphamvu, koma, inu mumapeza kuti, kulikonse kumene inu mupita, inu mumakapezako mzimu wa fuko.

<sup>182</sup> Inu mukapita ku tchalitchi ndipo mukamuwona m’busa, ngati iye ali wolusa kwenikweni ndipo amangopitirira, osonkhana amadzakhala chimodzimodzi. Mukuona? Iwo amatenga mzimu wa wina ndi mzake mmalo mwa Mzimu Woyera.



<sup>183</sup> Ndi chifukwa chake tiri ndi chiphunzitso chambiri chopotozedwa cha Baibulo. Mmalo mobwerera ku pulani, iwo atenga mzimu wa chipembedzo china. Mukuona? Koma Mawu ndi achilendo basi kwa iwo monga Iwo anali mmasiku amene Yesu anabwera, kulengeza Uthenga woona weniweni. Iwo anati, “Iye ndi mdierekezi. Iye ndi Belezebule.” Mukuona? Koma apo inu mukuzimvetisa izo.

<sup>184</sup> Ndipo iye anati, “Chabwino, ndiye, sitiri Achimerika, ndife chiyani?”

<sup>185</sup> Ine ndinati, “Ufumu wathu ndi wa Kumwamba.” Mwaona, ndife mfulu, obadwa mwatsopano. Ufumu wa Mulungu uli mkati mwako. Mwaona, zichitani ngati Kumeneko, ndinu nthumwi zochokera Kumeneko. Ine ndinati, “Ndife mbadwa kuno, tikukhala kuno mu thupi. Koma, mizimu yathu, ndife amwendamnjira ndi alendo.” Ndife achilendo kudziko lapansi tsopano, ngakhale fuko lathu lomwe, pakuti ife tavomereza kuitanidwa pamene kunagogoda pa mtima wathu, kuti tikhale gawo la Iye, Mawu Ake. Ndipo Mawu amatikonza ife, amatipanga ife kukhala moyo ndi kutipanga ife kumachita monga Akhristu.

<sup>186</sup> Nthawi ina kale, Kummwera, nkhani yaying’ono. Kunali mfumu. . . kapena, wogula. Iwo ankagulitsa akapolo. Izo zinali mu nthawi ya—a tsankho, ndipo iwo anali ndi akapolo Kummwera. Iwo anali a. . . Iwo ankapita ndi kukagula iwo, monga momwe inu mungachitire ndi galimoto yogwiritsidwa ntchito, kuichotsa kosungira.

<sup>187</sup> Tsopano, ndine woyanjanitsa, mwamtheradi. . . Ndikutanthauza wa tsankho. Ndine wa tsankho. Chifukwa, ine sindisamala momwe iwo akutsutsirana, inu simungakhale Mkhristu ndi kukhala woyanjanitsa. Ndiko kulondola ndendende. Mulungu amalekanitsa ngakhale mafuko Ake. Iye amawalekanitsa anthu Ake. “Chokanipo pakati pa iwo!” Iye ndi. . . Iye ndi wa tsankho. “Osati ngakhale. . . Musakhudze zinthu zawo zodetsedwa!” Iye anakoka Israeli, mtundu wa Chiyuda uja, kuchokera mu aliwonse, mafuko onse mdziko. Iye ndi wa tsankho.

<sup>188</sup> Koma ine sindimakhulupirira kuti munthu aliyense akuyenera kukhala kapolo. Mulungu anapanga munthu; munthu anapanga akapolo. Ine sindikhulupirira kuti wina ayenera kumamulamulira mzake, mtundu uliwonse, mtundu, kapena china chirichonse.

<sup>189</sup> Koma tsankho liripo, Mkwatibwi wa Khristu anasankhidwa kuchokera ku mipingo ina yonse, ndipo ndiko kulondola ndendende: mpingo wachibadwa, ndi Mpingo wauzimu; mpingo wachithupi, Mpingo wa Mawu. Izo nthawizonse zakhala ziripo. “Yesu anadza kwa Ake omwe, Ake omwe sanamulandire Iye; koma ochuluka amene anamulandira Iye!”

<sup>190</sup> Ndiye awa, anali ogula, ogulitsa amadutsa ndi kumagula akapolo awa. Nthawi ina kunali wina amene anabwera ku munda waukulu, ndipo iye ankawayang'ana iwo. Akapolowo ankamenyedwa mwamphamvu, ndi chirichonse, inu mukudziwa. Iwo anali kutali ndi kwawo; iwo sakanadzabwereranso kachiwiri. Ma Bhunu, achi Holland, anapita uko ndipo anakawatenga iwo, anawabweretsa iwo kuno ndipo amawagulitsa iwo. Ndipo iwo sadzawawonanso abambo kenanso, amayi kenanso, sadzawawonanso ana awo. Iwo ankawabalitsa iwo wina ndi mzake; ankasankha mwamuna wamkulu, kumubalitsa iye kwa mkazi wamkulu, kutali ndi mkazi wake yemwe, kuti apange akapolo aakulu. Oh, Mulungu adzawapangitsa iwo kuyankha tsiku lina! Uko nkulondola. Izo si zolondola.

<sup>191</sup> Monga Abraham Lincoln ananena nthawi ina, pamene iye anatsika bwato uko mu New Orleans, anavula chipewa chake chowoneka ngati paipi ya chitofu. . .

<sup>192</sup> Iye anaona achikuda atatu kapena anayi aang'ono, akubwera pansu, atayima pamenepo opanda nsapato, pamene iwo anali. . . Ng'ombe inali itagona ndipo imatenga—imachotsa chisanu pansu, iwo amayima atazithamangitsira ng'ombezo mkati. Mapazi awo aang'ono akale amaphulika, nkumawukha magazi. Iwo anali akuyimba, “Inu muli ndi nsapato, ine ndiri ndi nsapato, ndipo ana onse a Mulungu ali ndi nsapato.”

<sup>193</sup> Pamene iye anatsika mungalawayo kumusi uko, anayenda mpaka ku khola la ng'ombe, apo panali munthu wachikuda wamkulu atayima pamenepo, akumukwapula iye mozungulira, akuyesa mtima wake. Ndipo akumuthamangitsa iye chokwera ndi chotsika mu msewu, ndi chikwapu kumbuyo kwake; kenako nkuyeza mtima wake, kuwona ngati iye anali bwino. Mkazi wake wamng'ono wosauka atayima pamenepo, ana awiri kapena atatu ali mmanja mwake monga *choncho*; kuti amugulitse, kumukweranitsa iye kwa mkazi wamkulu. Abraham Lincoln wakale anayika izo pansu pa chipewa chake. . . chipewa chake pansu pa nkono wake, monga *choncho*, ndipo anamenya chibagera chake, iye anati, “Izo nzolakwika! Ndipo tsiku lina ine ndidzagunda izo, ngati izo zidzatengera moyo wanga.” Ndipo kutaliko, mnyumba yosungiramo zinthu zakale mu Chicago, muli diresi yokhala ndi magazi pa iyo, imene inamumasula munthu wachikudayo kwa izo.

<sup>194</sup> Ndipo ine ndikunena kuti tchimo ndi zinthu ndi zolakwika! Mulungu andithandize ine kuzigunda izo, ndi atumiki ena onse a Uthenga. Ife tinabadwa amfulu, ana a Mulungu. Ife tiribe ntchito ndi kachikhulupiriro kalikonse kapena gulu lampatuko kuti litipititse ife mu Bungwe la Mipingo Yamdziko. Ndife anthu obadwa mwaufulu, mwa Mzimu Woyera. Tiri ndi ufulu. Ife tinatuluka kuchokera mu zinthu zoterozo monga izo, kuti

tidzakhale achipentekoste. Uko nkulondola. Tsopano ndife amfulu. Sitikuyenera kumangika ku zinthu zimenezo kenanso.

<sup>195</sup> Koma wogula uyu anati, akuyang'ana pa akapolo ake, handirede kapena chinachake, a iwo, pa munda waukulu, iye anati, "Nnena!" Munthu wina wamng'ono pamenepo, iwo sankasowa kuti amukwapule iye; chidale chake panja, ndi chibwano chake mmwamba, ali pa ntchito! Anati, "Nnena! Ndikufuna kumugula iye."

<sup>196</sup> Iye anati, "Oh, ayi!" Mwiniwake anati, "Iye si wogulitsa. Huh-uh."

Iye anati, "Chabwino, kodi iye ndi kapolo?"

Anati, "Eya."

<sup>197</sup> Iye anati, "Chabwino, nchiyani chikumupangitsa iye kukhala wosiyana chotero?" Anati, "Kodi mumamudyetsa iye mosiyana?"

Iye anati, "Ayi, iwo onse amakadyera uko ku kitchini, pamodzi."

Anati, "Kodi iye ndi bwana wa iwo?"

Anati, "Ayi, iye ndi kapolo chabe."

"Chabwino," anati, "chimamupangitsa kusiyana ndi chiyani?"

<sup>198</sup> Anati, "Inu mukudziwa, ine ndinkadabwa izo, inemwini. Koma," anati, "inu mukudziwa, uko ku dziko la kwawo kumene iwo akuchokera, mu Afrika, abambo a mnyamata ameneyo ndi mfumu ya fuko. Ndipo ngakhale kuti ndi mlendo, iye amachita ngati mwana wa mfumu."

<sup>199</sup> Oh, ine ndimaganiza, ndi chinthu chotani kwa Chikhristu! Akazi, siyani kuvala zovala zimenezo monga choncho! Amuna, siyani kukamba nthabwala zachabechabe ndi zinthu zonsezo! Ndife ana aamuna ndi aakazi a Mfumu. Zivalani ngati mfumukazi, zivalani ngati a—dona. Muzichita ngati njonda, musalole kuti tsitsi lanu lizikula monga *chonchi*. Baibulo linati, "Ndi zolakwika (chirengedwe chimakuphunzitsani inu) kuti mwamuna akhale ndi tsitsi lalitali. Ndipo ndi chamanyazi ndi chinthu wamba kuti ngakhale mkazi azipemphera ndi tsitsi lake lometa." Nanga bwanji izi? "Ndi a—chonyansa kuti mkazi avale chovala choyenera mwamuna." Mulungu wamkulu wosasintha samasintha. Komabe lero ndi zomasuka basi monga fuko lathu lonse liriri. Manyazi! Tiyeni tizichita ngati ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Tiyeni tizikhala monga choncho. Ndife, ndife ana a Mfumu. Ife ndife. Ife ndife. Pakali pano gulu ili la chisokonezo ndi litsiro ndi nyansi, kuzungulira kuno, anthu amadzitcha okha "Akhristu" ndi kumachitabe monga choncho!

<sup>200</sup> Koma kumbukirani, ife tinapeza kugogoda tsiku lina, ndipo tinamutsegulira Iye kuti alowe, kunyada ndi zonse zinachokapo. Amen. Sindikusamala chimene iwo amanditcha ine!

Oh, ndikuganiza kuti ndangokhala wachikale,  
Koma Mpulumutsi wanga anali wachikale,  
nayenso.

<sup>201</sup> Nkulondola uko? Inu Munaimvapo nyimboyo. Mukhale achikale! Musamayesere kutengera winawake. Iye ndi Chitsanzo chanu. Muziyesetsa kukhala monga Iye, ndipo Mzimu mwa inu udzakuthandizani kuchita zimenezo. Muwupange moyo wanu kukhala monga Wake.

<sup>202</sup> Eya, pali chitseko pamenepo. Ndikufuna kutchula chitseko china. Ndimavulala kwambiri. Pali chitseko china pamenepo, pafupi ndi chitseko chimenecho, chikupita ku mbali ya kumanja, ndipo chitseko chimenecho ndi chitseko cha moyo wako wachinsinsi. Oh! Oh, inu simumafuna kuti Iye azisokonezako kumeneko. “Tsopano, ngati ine ndikufuna kuti ndipite ku phwando laling’ono la mowa, ndi chiyani kwa Inu? Ndi mpingo uti umene ungandiwuze ine chimene nditi ndichite?” Uh-huh, ndi zimenezotu pamenepo, mwaona. “Magawo teni a malipiro anga? Ndani ati andiuze ine choti ndichite? Umenewo ndi moyo wanga wachinsinsi! Ndimapanga ndalama izi. Ndiri ndi moyo wanga wanga. Ndimavala akabudula ngati ndikufuna. Uwo ndi mwayi wanga wanga waku America.” Izo nzoona. Ndithudi. Kulondola.

<sup>203</sup> Koma ngati ndiwe mwanawankhosa, ndipo osati mbuzi, mwaona, anaankhosa ndi chimene Iye akufuna. Iwo adzalekanitsidwa tsiku lina.

<sup>204</sup> Nkhosa ili ndi ubweya. Ndicho chinthu chokhacho chimene iyo ili nacho. Ndipo iyo singathe kupanga ubweya umenewo. Ife sitipemphedwa kupanga chipatso cha Mzimu, koma kuti *tizibala* chipatso cha Mzimu. Ndipo bola ngati ili nkghosa, iyo idzabala. Iyo simasowa kupanga. Zokhudzira ndi chirichonse mwa iyo ndi nkghosa, iyo imapanga ubweya chifukwa mkati mwake muli zokhudzira ndi ndulu ndi zinthu zimene zimafunika kupanga ubweya.

<sup>205</sup> Ndipo pamene iwe ukhala Mkhristu, iwe umagwirizana ndi Mawu. Sindikusamala chimene wina aliyense akunena. Iwe sumasowa kuchita kalikonse, ndi kugwetsa kalikonse, kukoka, kupopera mmwamba. Ndiwe Mkhristu. Iwe mosadzipangitsa umangobala chipatso cha Mzimu. Mukuona? Mwaona, ndipo umo ndi momwe izo zimakhalira. Mukuona?

<sup>206</sup> Koma, anthu lero, samafuna kuti udzisewera ndi moyo wawo wa mseri.

<sup>207</sup> Chinthu chokha chimene mungachite, mungotsegula chitseko chirichonse pamenepo, tsopano ndikuti, “Dzaloweni, Yesu.” Mupenye chimene chingachitike. Pamene inu muwona mu Bukhu, inu mukuyenera kuti muchite *ichi*, inu muchite icho. Chifukwa chiyani? Ndinu nkghosa, kuyamba ndi kuyamba, pamenepo.

208 Koma ngati mukungofuna kuti mukhale, kumusunga Iye pa chitseko, kungoti, “Ndajowina tchalitchi. Ndine wabwino basi monga inu. Mwaona, ine ndinamulandira Khristu.” Mwinamwake ndi chimene inu munachita. Koma kodi inu munamupanga Iye *Ambuye*? Mukuona?

209 Tsopano, Ambuye sangakhalire pansi Bukhu la malamulo ndi kunena Mawu, ndipo kenako nkubwera apo nkudzawakana Iwo. Ndipo ngati inu munena kuti muli nawo Mzimu Woyera, ndipo Baibulo nkumanena chinthu chinachake choti muchite, ndipo inu nkuti, “Oh, ine sindimakhulupirira *Izo*.” Inu mungokumbukira, mzimu umenewo mwa inu si Mzimu Woyera, chifukwa Iye sangazikane Yekha. Uko nkulondola. Iye sangazikane Yekha. Iye analemba Mawu, ndipo Iye amawayang’anira Iwo, kuti awachite Iwo. Mukuona? Chotero si Woyera. . .

210 Ndi mzimu, chabwino. Ukhoza kukhala a—mzimu wa mpingo. Iwo ukhoza kukhala mzimu wa m’busa. Ukhoza kukhala mzimu wa dziko. Iwo ukhoza kukhala. Ine sindikudziwa chimene icho chiri, koma, chirichonse chimene icho chiri, iwo ukhoza kukhala mzimu wachipembedzo, “Ndine wa Methodist. Ndine wa Baptisti. Ndine wa Presbateria. Ndine wa Pentekoste. Ndine *ichi*.” Ndizo Pentekoste.

211 Tsopano kumbukirani, ndiloleni ine ndiziwongole zimenezo; pentekoste si bungwe, pentekoste ndi chokuchitikirani chimene inu mumalandira. Inu Amethodisti, Abaptisti, Akatolika, ndi onse, mukhoza kukumana nayo pentekoste. Inu simungajowine pentekoste, chifukwa palibepo njira yojowinira iyo.

212 Ine ndakhala mu banja la a Branham kwa zaka fifite-faivi. Inu mukudziwa, iwo sanandifunse konse ine kuti ndikhale Branham. Ine ndinabadwa, ndiri Branham.

213 Ndipo umo ndi momwe iwe umakhalira Mkhristu, iwe umabadwa uli Mkhristu. Izo nzoona, tsopano.

214 Oh, moyo wamseri umenewo! “Oh, ine ndikukuuzani inu, abusa anga amapita ku zovina izi, ndipo ife timachita gwedemula. Iwo ali nacho.” Chabwino. Mukuona? “Musabwere kudzandiuza chimene ndingachite komanso chimene sindingachite.” Chabwino, mwaona, inu simungamulole Iye kuti alowe.

215 Mungomulola Iye alowe nthawi imodzi, ndipo kenako nkubwereranso ku zovina kapena gwedemula, kapena chirichonse chimene inu muti muchite, muwone chimene mungachite. Inu simungathe kuchita izo. Mudzamulole Iye adzalowe nthawi imodzi, ndipo kenako mudzayambe kuvala akabudula, ena a inu akazi.

216 Ndikudziwa kuti ndikukutengerani nthawi yayitali, koma ndikufuna kunena chinthu chimodzi china, ngati ziri bwino, pa nkhani iyi.

217 Ine ndikuganiza, msonkhano waukulu kwambiri umene Ambuye anandilora ine kuti ndimuchitire Iye unali mu Bombay, kumene ndinali ndi faivi handirede sauzande, koma, ndi thuu handirede ndi masauzande angapo mu—mu Afrika, Durban, pa bwalo la mpikisano. Masana amenewo, ine ndinati, iwo atatha kuwona chinthu chachikulu chodabwitsa chotero chimene Ambuye wathu wachisomo anatsika pansi ndi kudzachichita, Ine ndinati, “Amishonare anakuphunzitsani inu Mawu, koma Mawu amafulumizitsidwa ndi kupangidwa amoyo. Chimene iye amanena chikuyenera kukhala chamoyo.” Ndipo—ndiyeno pamene panali machiritso twente-faivi sauzande akuchitika pa nthawi imodzi, ndi mulu pambuyo pa mulu wa mipando yabwino yakale kumeneko; pemphero laling’ono limodzi lophweka, iwo anali atawona Mzimu Woyera basi... Anthu amenewo omwe sankadziwa nkomwe chimene iwo anali ndi kumene amachokera, ndizo zonse zimene iwo ankafuna kuti awone. Mukuona?

218 Ndipo ine ndinafunsa, “Ndi angati akufuna kuti amulandire Khristu?” Apo panali sarte sauzande atayima pa mapazi awo, mbadwa zamabulangete, atanyamula mafano.

219 Dokotala Bosworth, Dokotala Baxter ndi iwo, anayamba kulira. Ndipo M’bale Bosworth anathamangira uko, anati— anati, “M’bale Branham, ili ndi tsiku lanu lovekedwa korona.”

220 M’bale Baxter anati, “M’bale Branham, ine ndikudabwa, ine ndikuganiza iwo amatanthauza machiritso athupi.”

221 Mnyamatayo anali mmanja ndi mawondo ake. Ndipo Mzimu Woyera unamuuzza iye kumene iye amachokera, chimene chinali chitachitika, unati, “Iwe uziyankhula. Ukuganizira za m’bale wako, ali pafupifupi theka la mailo kumbuyo uko. Iye amakwera mbuzi yachikasu, ndipo anavulaza mwendo wake.” Ine ndinati, “Koma, PAKUTI ATERO AMBUYE, iye wachiritsidwa.” Apa panabwera mnyamatayo, ali ndi ndodo mmanja mwake, monga *choncho*. Ndipo zinawatengera iwo pafupifupi mphindi twente kuti gulu la asirikali liwatontholetse iwo.

222 Ndiye mnyamata uyu, mmanja ake ndi mapazi, monga *choncho*, pansi, samatha ngakhale kuimirira, wamaliseche. Oh, mai, chinthu choyipa chotero! Iye ankaganiza kuti iye amabwera kumeneko kwa alendo, inu mukudziwa, kuti adzakhale ngati akuchita a—kuvina mnkhalango. Ndipo ine ndinatenga chingwe ndipo ndinachigwedeza icho. Ine ndinati, “Ngati ndingathandize cholengedwa chosawuka icho, ndipo osachita icho, ine ndingakhale a... Sindingakhale woyenera kudzaima kumbuyo kuno. Koma,” Ine ndinati, “Sindingathe kumuthandiza iye. Koma tsopano ndiri ndi mphatso yaying’ono, ine ndikhoza kungoyikoka iyo mu giya, chirichonse chimene Ambuye ati anene.”

223 Ndipo pamene Ambuye anawonetsera, anamuuya iye chimene iye anali, anati, “Amayi ake ndi abambo akhala kunjia uko, iwo ndi Achizulu.” Ndipo anati, “Iwo ndi ochepa thupi, mwachirendo.” Mzulu amalemera pafupifupi mapaundi firii handiredede, munthu aliyense. Chotero ndiye anati, “Iwo ndi achirendo. Koma mnyamata uyu anabadwira mnyumba ya Chikhristu, chifukwa pa ake...kudzanja lamanja, pamene ukukalowa pa chitseko, pali chithunzi cha Khristu, mu kanyumba kakang’ono kaudzu.” Ndipo izo zinali zoono ndendende. Amayi ake ndi abambo ake anadzuka. “Ndipo *limenelo* ndi dzina lawo.” Ndi chimene iye anali, ndi chirichonse. Iwo sanathe kumvetsa. Ine ndinayang’ana mmbuyo ndipo ine ndinamuwona iye atayima, mmasomphenya apo, mowongoka basi monga iye akanathera. Sanadzukepo nkomwe, mmoyo wake, iye anabadwa ali chomwecho. Ine ndinati, “Ambuye Yesu amuchiritsa iye.”

224 Iye sanali ngakhale mmalingaliro ake abwino, akuyesera kuti azipita, “uh, ba, ba, ba,” monga choncho.

225 Ndipo ine ndinagwira chingwecho, ndipo ndinachigwedeza icho monga *choncho*. Ine ndinati, “Yesu Khristu, mwana, wakuchiritsa iwe. Imirira pa mapazi ako.” Pamenepo iye anadzuka. Misozi ikuyenderera pansu, ndi pa mimba yake yakuda, pamene iye ankapita akuyenda monga choncho. Ine ndinawona mbadwa zamabulangete sarte sauzande zikupereka mitima yawo kwa Yesu Khristu.

226 Ndiri ku Kiwanis Club, ndinanena tsopano...Ndipo iwo anandiuza kuti ndidza “khala woyera wodzigudubuza” pamene ndinkachoka mu mpingo wa Baptisti, kuti ndizisonkhana ndi anthu onse. Iwo anati, “Chabwino, mudzakhala woyera wodzigudubuza,” Ine ndinakhala. Gulu la abale anga Achibaptisti linatero. Ine ndinati, “Inu mwatumiza amishonare kumeneko, kwa zaka handiredi ndi fifite zapitazo, kodi ine ndinawapeza iwo chiyani? Akunyamulabe mafano.” Ine ndinati, “Koma mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu, sarte sauzande analandira Khristu pa nthawi imodzi.”

227 Tsopano ine ndikufuna kuti ndinene kwa inu akazi, inu mukudziwa chimene chinachitika kwa akazi amenewo? Ine ndinati, “Pamalo omwewo amene inu mwaimapo, Mzimu Woyera ukudzazani inu.” Ndipo pamene iwo anakweza manja awo kuti amulandire Khristu ngati Mpulumutsi wawo, ndipo pamene iwo anayenda kuchoka pamenepo; amaliseche, tsopano, opanda kanthu koma kachigamba kakang’ono chabe, kosoka, kutsogolo. Ndipo pamene iwo anachoka pamenepo, iwo anapinda manja awo monga *chonchi*, chifukwa iwo anali mu kukhalapo kwa mwamuna, iwo atatha kumulandira Khristu.

228 Tsopano ife tingathe bwanji, alongo, ife tingathe bwanji mu fuko lino limene ife timadzinenera kuti timakhulupirira

ndi kukhala Akhristu, ndipo chaka chirichonse iwo amachotsa zambiri? Pamene, munthu ameneyo sanamve nkomwe Dzina la Khristu, koma anangomulandira Iye mu mtima mwawo. Ayi, sukanawauza iwo kuti iwo anali amaliseche, iwo sankadziwa izo. Koma iwo anadziphimba okha monga *chonchi*, kuti achokepo. Tsiku lotsatira, kapena awiri, umawapeza iwo atavala zovala, zamtundu wina. Oh, mai!

<sup>229</sup> Pali chinachake cholakwika penapake. Ndi kupotoza kwa fioloje. Mphamvu ya chiukitsiro cha Yesu Khristu, monga Iye anachitira kwa munthu amene ankatchedwa “Legiyo,” ife tinamupeza iye atavala ndipo ali mmalingaliro ake abwino. Ndipo ine ndinayamba kukhulupirira kuti ndi mzimu pa anthu umene umawatsogolera iwo mu Chimerika chimenecho ndi Chifaransa, ndi mitundu yonse ya chidziko ndi chitchalitchi. Koma aloleni iwo kamodzi abwere kwa Ambuye ameneyo, ndipo iwo amverere kugogoda uko pa chitseko, iwo avala zovala ndi kumachita monga akazi ndi amuna, ndipo iwo akhala Akhristu obadwa mwatsopano. Amen. Inde.

<sup>230</sup> Tsopano ndatsiriza, maminiti twente kuti ikwane thwelofu, basi—maminiti pang’ono, ndiloleni ine ndilambalale zina. Mphindi chabe, Malemba ena, ine ndikufuna kuti nditsegule chitseko chimodzi chowonjezera. Kodi izo zingakhale bwino?

<sup>231</sup> Khomo lotsatira, kupita kumeneko, ndi chikhulupiriro. Mwaona, moyo wanu wamseri. . . khomo la kunyada, moyo wanu wamseri, tsopano tiyeni titsegule chikhulupiriro. Mkombero wonse wa iwo, mwaona, koma tiyeni tipite mu chikhulupiriro.

<sup>232</sup> Inu mukudziwa, nthawi ina kalelo ine ndinali mu chipatala ndipo mkazi akupita ku oparehoni. Iye anandiyimbira, iye anati, “M’bale Branham, ndine wobwerera m’mbuyo. Kodi mungandipempherere ine?”

<sup>233</sup> Ine ndinati, “Inde, amayi, ndingakhale wokondwa kutero.” Ine ndinati, “Ndiwe wobwerera mmbuyo?”

“Eya.”

<sup>234</sup> Ine ndinati, “Tsopano tiyeni tingodikirira miniti yokha. Ndiloleni ine ndikuwerengereni Malemba.”

<sup>235</sup> Uko kunali dona atagona pamenepo pa bedi, anandiyang’ana ine, mwachirendo kwenikweni; iye, ndipo mwana wake wamwamuna pafupifupi usinkhu wa zaka twente, Ricky wachizolowezi, ndipo atayima pamenepo akuyang’ana pa ine monga choncho.

<sup>236</sup> Ndipo ine ndinati, “Inde, amayi,” Ine ndinati. Ndinamuwerengera iye Malemba, “Ngakhale machimo anu ali ofiira, adzakhala oyera ngati matalala. Ngakhale atakhala ofiira ngati kapezi, adzakhala oyera ngati ubweya.” Ndipo pamene ine ndinamuwerengera izo, ine ndinati, “Ngati iwe wasochera kutali, waona, iwe unachoka kwa Mulungu, koma



Mulungu sanachoke kwa iwe, kapena iwe sibwenzi ukundiyyitana ine.” Iye anayamba kulira. Ine ndinati, “Ife tipemphera.”

<sup>237</sup> Dona ameneyo pa bedi lotsatira, anati, “Dikirani miniti! Dikirani miniti pamenepo!”

Ine ndinati, “Inde, amayi?”

Iye anati, “Kokani katani imeneyo!”

Ndipo ine ndinati, “Kodi inu si Mkhristu?”

Iye anati, “Ndife a Methodisti!”

<sup>238</sup> Ine ndinati, “Chabwino, izo ziri ndi chochita chanji ndi zimenezo? Mwaona, izo sizochuluka kuposa kunena kuti iwe unali a—iwe unali mwana wa bulu, ngati iwe unali mu khola la nkumba, mwaona.” Ine ndinati, “Izo sizikutanthauza kanthu.” Mukuona?

<sup>239</sup> Koma, inu mwaona, ndi pamene izo zabwera, kudzilungamitsa nokha kumeneko. “Izo ndizotsutsana ndi chikhulupiriro chathu!” Ine ndinati... “Ife sitikufuna machiritso Auzimu mu mpingo wathu, kapena mtundu umenewo wa zinthu.” Mwaona, mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mwaona, iwo sangalole kulowa chitseko chimenecho. “Izo ndi zotsutsana ndi chikhulupiriro chathu.”

<sup>240</sup> Pali Chikhulupiriro chimodzi chokha. “Chikhulupiriro chimodzi, Ambuye mmodzi, ubatizo umodzi.” Chikhulupiriro chimenecho!

Chikhulupiriro changa chikuyang’ana kwa

Inu,

Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,

Mpulumutsi Waumulungu;

Tsopano ndimveni pamene ndikupemphera,

Chotsani kusakhulupirira kwanga konse,

<sup>241</sup> Tchimo! Tchimo, liripo tchimo limodzi lokha, ndiro kusakhulupirira. Munthu amene amamwa si wochimwa. Mwaona, izo—izo—izo, mwaona, si tchimo. Si a—si tchimo kumwa. Si tchimo kuchita chigololo. Kunama, kuba, izo si tchimo. Izo ndi zikhumbo za kusakhulupirira. Ngati inu mukanakhala okhulupirira, inu simukanachita zimenezo, mwaona.

<sup>242</sup> Pali awiri okha, ndiwe wosakhulupirira kapena wokhulupirira, mwaona, mmodzi kapena winayo. Inu simumachita zinthu zonsezi ndi madongosolo achipembedzo monga choncho, chifukwa choti ndinu wosakhulupirira; ngati iwe uli wokhulupirira, ndi Mawu amene iwe umawakhulupirira, chifukwa Khristu ndi Mawu. Mukuona? Ndipo chotero ndiwe wosakhulupirira basi chifukwa umakhulupirira miyambo ina, kapena nthano zina zimene zawonjezedwa ku Baibulo, kapena chinachake, ndi zipembedzo zimachita. Koma wokhulupirira weniweni amakhalabe molondola ndi Mawu amenewo. Ndipo

Mulungu amagwira ntchito kupyolera mu Mawu amenewo, kupyola kumene kuti awapange Iwo kukwaniritsidwa, mu kam'badwo kano kamene ife tikukhalamo.

<sup>243</sup> Ndipo tsopano zindikirani, ndipo inu mukuti, “Oh, ine . . . M'bale Branham, Ambuye . . .” Chabwino, izo ziri bwino, uko kunali Afilisiti ambiri osadulidwa anapita nthawi ina, nawonso. Ndipo gulu la Aigupto linayesera kumutsatira Mose kuwoloka—Nyanja Yofiira, koma izo potsiriza . . . “Monga Yane ndi Yambre anamutsutsa Mose, chabwino, ife tikupeza chinthu chomwecho mu tsiku lotsiriza,” Baibulo linatero.

<sup>244</sup> Tsopano mopitirira pang'ono. Yesu ananena apa, mu uwu—m'badwo uno, “Chifukwa inu mukunena kuti, ‘Ndine wolemera, ndipo ndine wochulukira mu zinthu.’” Tangowonani momwe ife tiriri lero, mpingo wolemera kwambiri umene unayamba wakhhalapo! Ndipo, chabwino, inu mukudziwa, inu Achipentekoste mukanakhala bwino ngati inu mukanakhala kunja uko ndi nkhotcho, pa ngodya, monga abambo ndi amayi anu anali. Koma inu muli ndi matchalitchi abwinoko kuposa ena onsewo tsopano, okula mofulumira kwambiri mdziko; koma kodi uli kuti Mzimu wa Mulungu uja umene unakakhala pakati pathu? Inu munachisiya chinthu chenicheni. “Chifukwa inu mukuti, ‘Ndine wolemera.’”

<sup>245</sup> Kumbukirani, ichi ndi Chipentekoste chimene chikuyankhula, chifukwa m'badwo wa Chipentekoste ndi m'badwo wotsiriza. Mwaona, chitsitsimutso chonsechi chimene ife takhala nacho, palibe bungwe lina likuyamba. Apo sipadzakhalapo. Awa ndi mathero. Tirigu wakhwima tsopano. Iye wabwera kudutsa mmasamba, ndi phesi, ndi mankhusu, ndipo iye watulukira kupita ku tirigu tsopano. Mwaona, sipakhalanso zochulukira. Iwo anayambitsa Mvula ya Masika yaing'ono, koma iyo inangogwera mkati momwe; china chirichonse chidzatero. Iwo adzatero. Uyu ndi tirigu amene akubwera. Zindikirani.

<sup>246</sup> “Ndipo chifukwa inu mukuti, ‘ndine wolemera, ndi wochulukidwa mu chuma, wosasowa kanthu,’ ndipo simudziwa kuti inu ndi omvetsa chisoni, atsoka, akhungu, amaliseche, ndipo simukudziwa; Ine ndikukulangizani inu . . .” Oh, mai! “Ine ndikugogoda pa chitseko chanu.” [M'bale Branham akugogoda pa chinachake—Mkonzi]. “Laodikaya, Ine ndikugogoda pakhomo pako, ndi kukulangiza kuti ubwere kwa Ine, ndi—ndi kudzagula golide woyonedwa mu moto; zovala zoyera, kuti umaliseche wako usawonekere.”

<sup>247</sup> Chotsani zinthu izi, ndipo uvala monga iwe ukuyenera kuvalira, mwaona, chirungamo cha Khristu, Mawu. Osati chirungamo changa; Chirungamo chake!

<sup>248</sup> “Ndipo inenso ndikulangiza iwe kuti—kuti ubwere udzatenge mankhwala a mmaso, kuti ukakhoze kudzoza

maso ako, kuti uthe kupenya. Mankhwala a mmaso!”

<sup>249</sup> Ndine waku Kentucky. Ine ndinabadwira kumusi kumapiri, ndipo ife tinali ndi malo akale aang’ono pamwamba mu chipinda chapamwamba. Ndipo ife ana tinali titayika—makwerero a mtengo akale, amene ife tinkakwerera usiku uliwonse. Ndipo tinkakagona. Iwo ankayenera kuika chinsalu pamwamba pathu kukagwa chisanu. Chabwino, nyenyezi, matabwa akale. . .

<sup>250</sup> Ndi angati amadziwa chimene matabwa ali? Chabwino, m’bale, chifukwa chiyani ine sindinavale ovololo yanga pamwamba apa? Ine ndiri kwathu ndithudi, mwaona. Chabwino, matabwa akale!

<sup>251</sup> Ndi angati amadziwa chimene mkeka uli? Tsopano mumadziwa chiyani! Ine ndimaganiza kuti ndamverera mwachipembedzo kwambiri pa chinachake. Chabwino, ndikuganiza kuti ndiri kwathu tsopano. Izo nzabwino. Ndipo ine sindimadziwa nkomwe kalikonse mpaka zaka zingapo zapitazo.

<sup>252</sup> Ndi angati amadziwa chimene nyali yakale ili, chumuni chakale, mukudziwa? Umenewo unali mwezi waukulu wakale, ndi kadzidzi pambalipa. Iwo anali ndi dzanja laling’ono kwambiri mnyumbamo, amayenera kuyeretsa chipwirikiti chakale icho, inu mukudziwa. Ine ndinkachita kutenga chowazira chakale, ndipo icho chonse chimawaza pa ine; chotero ine ndinatenga nyali imeneyo ndipo ndinaitembenuzira iyo pamenepo, kuti isawazidwe. Inde, ndithudi.

<sup>253</sup> Tsopano, agogo anga aamuna anali otchera misampha. Amayi a amayi anga amachokera ku malo osungirako. Iwo anakwatira mtsikana wa ku India wochokera ku malo osungirako aku Cherokee uko ku Kentucky ndi Tennessee, inu mukudziwa kumene, chigwa cha Cherokee. Ndipo, iwo, iwo—iwo ankasaka ndi kutchera misampha, nthawi zonse, izo zinali—umo ndi mmene iwo ankakhalira moyo.

<sup>254</sup> Ndipo ife ana titagona pamenepo, bwanji, nthawizina kumazizira kwenikweni. Ndipo kamphepo kameneko kakubwera kudutsa pamenepo, ife timayamba kuzizidwa mmaso mwathu, ndipo—ndipo maso athu amatsekeka usiku, inu mukudziwa. Amayi ankazitcha izo “manthongo.” Ine sindi—sindikudziwa chimene icho chiri, koma kuzizira kumafika mmaso mwanu, ndipo iwo amazizidwa. Ndipo iwo amakhoza kunena kuti, “Muli ndi manthongo mmaso mwanu,” chifukwa cha—cha, inu mukudziwa, mphepo ikuwomba kudutsa pamenepo, mpemera umabwera kudzadutsa usiku. Maso athu amatupa nkutsekeka.

<sup>255</sup> Ndipo amayi amakhoza kufika pamenepo pa makwerero, mmawa, pamene iwo anali atapanga mabisiketi. Iwo ankakhala ndi manyuchi a mapira atayikidwa pa tebulo. Ndipo iwo amakhoza kunena, “Billy!”

Ine ndinkati, “Inde, amayi?”

“Iwe ndi Edward bwerani pansu.”

<sup>256</sup> “Amayi, sindikutha kupenya!” Ndinkamuyitana mchimwene wanga, ife tinkamutcha iye, “Humpy.” Ine ndinati, “Iye sakutha kupenya, nayenso. Mwaona, maso athu anali ali ndi manthongo mwa iwo.”

Iye ankati, “Chabwino, miniti yokha.”

<sup>257</sup> Ndipo agogo, pamene iwo amakhoza kugwira kanyimbi. Ndi angati akudziwa chimene kanyimbi ali? Ndicho chimene, ndipo iwo ankati. . . Iwo ankagwira kanyimbi, ankachotsa mafuta pa iye ndi kumuyika mu chitini. Ndipo mafuta a kanyimbi amenewo anali mankhwala mu banja mwathu. Iwo ankatipatsa ife iwo chifukwa cha chimfine choyipa, chokhala ndi phula pamene, ndi mafuta amakala. Ife tinkazimeza izo chifukwa cha zilonda zapakhosi. Kenako tinkatenthetsa mafuta a kanyimbiwo, iwo ankabwera ndi kudzatikitira mmaso mwathu, ndipo maso athu ankatseguka. Mwaona, anali mafuta a kanyimbi amene ankachita izo. Mukuona?

<sup>258</sup> Tsopano, m’bale, mlongo, ife tadutsapo mu nyengo yozizira, mu mpingo. Ndiko kulondola, zolemba zambiri zachipembedzo zadutsapo, aliyense wagwidwapo ndi chimfine. Anthu ambiri zatseka maso awo, ndipo pali Bungwe lalikulu la Mipingo ya Mdziko lonse limene likubwera, pamwamba apa, lidzakakamiza aliyense wa inu kulowa mu ilo. Iwo akuchoka ku Mawu amenewo, magulu athu omwe akutero. Ine ndi wokakamizika ku Uthenga; osati kuti ndikhale wosiyana, koma chifukwa cha chikondi. Chikondi chimakonza. Bwererani! Khalani kutali ndi chinthu chimenecho! Inu abale otumikira, ine sindikusamala chimene magulu anu amachita, khalani kutali ndi izo! Khalani kunja kwa izo! Icho ndi chilemba cha chirombo, khalani kutali ndi icho! Mwaona, Yesu akugogoda mu m’badwo wa Laodikaya uno. Mukuona kumene iwo amutulutsako Iye? Iye akuyesetsa kuti afikire kwa munthu payekha, osati—osati mabungwe ndi magulu a anthu. Iye akuyesetsa kuti amutenge mmodzi *apa*, ndi wina *apo*, ndi wina *apo*, akuyesetsa. “Onse amene Ine ndimawakonda, ndimawalanga.”

<sup>259</sup> Monga m’bale wamng’ono yo anali ndi masomphenya apa, ndipo anati iye anali ndi masomphenya. Ndipo anati, “Kuwala komweko kumene inu mukukulandira, kumayambitsa imfa yanu, inunso.” Mukuona?

<sup>260</sup> “Ochuluka amene Ine ndimawakonda, Ine ndimawalanga; khalani achangu, ndipo mubwerere. Ndayima pakhomo, ndipo ndikugogoda.” Tsopano, penyani, mafuta a kanyimbi sangachite ubwino uliwonse.

Koma kuli Kasupe wodzaza ndi Mwazi,  
Wochokera mmitsempha ya Emmanuele,

Kumene ochimwa akagwera pansi pa  
kusefukirako,  
Amataya mawanga onse a zolakwa zawo.

Wakuba wakufa uja anakondwera kuwona  
Kasupe uja mu tsiku lake;  
Pamenepo ine, ngakhale woyipa ngati iye,

<sup>261</sup> Iye anatsegula maso anga, ndi mankhwala Ake opaka mmaso. Mzimu Wake unatsika ndipo unadzathethetsa Baibulo, mankhwala Ake opaka mmaso. Ine sindimatha kupenya Iwo. Ine ndinali wa wamba, m'busa wa Baptisti. Koma tsiku lina Iye anatumiza Mzimu Wake pansi, osati mafuta a kanyimbi Iye anawatenthetsa, koma Iye anatumiza Mzimu Woyera ndi moto! Mankhwala opaka mmaso apang'ono anapukuta pa Baibulo langa—Mabaibulo anga...ndipo ndikutha kupenya ndi diso langa, Ndikutanthauza anapukuta mmaso mwanga kuti ndithe kupenya Baibulo langa. Ndipo ine ndinawona kuti, "Iye anali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale owona. Ine ndayima pa chitseko, ndipo ndikugogoda."

<sup>262</sup> Nkhani imodzi yaying'ono yowonjezera. Kodi ife tiri ndi nthawi? Eya, eya, kenako ndizipita, mwaona.

<sup>263</sup> Kunali munthu wakuda wakale kumusi uko Kummwera. Ndipo, abusa ake, ine ndinkawadziwa iwo, munthu wabwino wachikulire. Iye tinkamutcha iye Gabe. Dzina lake linali Gabriel, ndipo tinkangomutcha iye kuti Gabe. Iye nthawizonse, abusa ndi ine, ife—ife tinkapita kokasaka, mochuluka kwambiri. Iye anali m'bale wachikulire wachikuda, ndipo ife tinkapita uko kukasaka. Ndipo chotero Gabe wokalamba anakonda kusaka bwino kuposa aliyense amene ine ndinamudziwapo, koma iye anali wosawombera bwino. Chotero, tsiku lina abusa ake ndi iye anapita kokasaka.

<sup>264</sup> Ndipo sitinkatha kumupangitsa Gabe wokalambayo kuti apite ku tchalitchi. Iye basi samachita zimenezo. Iye samabwera ku tchalitchi. Iye ankati, "Ah, Ine sindimapita kumusi uko kumene kuli achinyengo."

<sup>265</sup> Ine ndinati, "Koma, Gabe, bola ngati iwe ukukhala kunja, iwo ndi aakulu kuposa iwe. Iwe ukubisala kumbuyo kwa iwo, mwaona." Ine ndinati, "Iwe ukubisala kumbuyo kwawo. Ndiwe wamng'ono kuposa iwo; iwo amapita ndi kukayesetsa, mwaona."

<sup>266</sup> Ndipo chotero iye anati, "Ine—ine—ine—ine—ine ndimaganza zochuluka za inu, Bambo Bill. Koma," anati, "Ine—ine—ine—ine ndikudziwa Jones wokalamba amapita kumeneko, ndipo iye si kanthu; iye amasewera juga, ndi zonsezo."

<sup>267</sup> Ine ndinati, "Izo zonse nzabwino, Gabe. Mwaona, izo zonse nzabwino. Koma, kumbukirani, Jones akuyenera adzayankhire zimenezo; iwe sukuwera kudzatero, mwaona."

Ngati iwe ungapite...” Ine ndinati, “Iwe uli ndi m’busa wabwino.”

268 “Oh, M’busa Jones ndi mmodzi wa anthu abwino kwambiri amene alipo mdziko muno!”

269 Ine ndinati, “Ulole iye akhale chitsanzo chako, ngati sungathe kuyang’ana patali kuposa pamenepo. Ulole iye akhale chitsanzo chako.”

270 Chotero tsiku lina M’bale Jones anati, anamutenga Gabe wokalamba kokasaka, ndipo anati, “Ife tinagwira akalulu ndi mbalame zambiri, tsiku limenelo, kuposa momwe ife tikanatha kuzinyamula.” Ndipo anati, “Mubwere madzulo.” Anati, “Gabe wokalamba anali akubwera kumbuyo, ndipo onse ataledwa, inu mukudziwa, monga choncho.” Ndipo mkazi wake anali Mkhristu weniweni, wokhulupirika. Iye anali ndi malo pamenepo, mkazi wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo iye nthawizonse amakhala ndi malo ake a ntchito. Chotero iye anali... Gabe wokalamba anali akubwera mmbuyo, inu mukudziwa. Ndipo M’busa Jones anati iye anayang’ana mozungulira, iye amakhoza kuwona, “Gabe wokalamba anapitirira kumayang’ana pa phewa lake, monga *choncho*. Dzuwa likulowa,” anati, “likutsika kwenikweni, kukuyamba kuzizira.” Anati, “Patapita kanthawi,” anati ankayenda limodzi, anati, “Gabe wokalamba anabwera. Iye anali ndi mkombero wa mfuti yake wodzaza ndi akalulu ndi mbalame, ndi zinthu.” Anati, “Iye anawagwira abusa paphewa, ndipo anati, ‘Abusa?’”

Anati, anatembenuka, anati, “Eya, Gabe, chavuta ndi chiyani?”

271 Chotero iye anayang’ana, ndipo misonzi yaikulu ikuyenderera kuchokera mmasaya ake akuda, pamene ndevu zake zinali zikuyamba imvi. Iye akuti, “Abusa, Ine ndakhala ndikuyenda mu gombe ili kuno, kwa pafupifupi theka la ora.” Anati, “Ndakhala ndikupenya dzuwa limenelo likukalowa.” Anati, “Mukudziwa, ndevu zanga za imvi izi, ndipo tsitsi langa likusintha,” anati, “mukudziwa, dzuwa langa likulowanso, abusa.”

272 Anati, “Ndiko kulondola, Gabe.” Ndipo iye anangoyima ndi kutembenuka, anati, “Chavuta ndi chiyani ndi iwe?”

273 Iye anati, “Dzuwa langa likulowa, nanenso.” Iye anati, “Inu mukudziwa chiyani?” Anati, “Ndinayamba kuganiza,” iye anati, “pamene ine ndinkayenda motsatira kumbuyo uko.” Iye anati, “Inu mukudziwa,” anati, “Ambuye ayenera kuti amandikonda ine.”

Anati, “Ndithudi, Iye amatero, Gabe.”

274 Anati, “Inu mukudziwa, ndine wosatha kuwombera bwino.” Anati, “Sindinathe kuwombera kalikonse, koma,” anati, “ife—ife timaifuna kwambiri nyama imeneyi kunyumba.” Ndipo anati,

“Tangoyang’anani pa gulu labwino lalikulu la nyama limene Iye wandipatsa ine, mbalame izi ndi akalulu awa.” Iye anati, “Ine ndiri ndi zokwanira kutisunga ife tonse sabata yamawa.” Anati, “Iye ayenera kuti amandikonda ine, chifukwa ine sindingathe kuwombera kalikonse, inu mukudziwa.” Anati, “Ine sindinathe kuwombera iyo, koma tangowonani zimene Iye wandipatsa ine.” Kenako iye anati, “Iye ayenera kuti amandikonda ine, kapena Iye sakanandipatsa ine izi.”

Anati, “Uko nkulondola.”

<sup>275</sup> Ndipo iye anati, “Chabwino, ine ndinali ndi kugogoda kwachirendo pa chitseko changa, kumusi uko. Iye anandiuza kuti nditembenuke, anati, ‘Gabe, dzuwa lako likulowa, nawenso.’” Anati, “Abusa, inu mukudziwa chimene ine ndachita, abusa?” Iye anati, “Ine ndinamupangira Iye lonjezo.”

<sup>276</sup> Iye anati, “Gabe, ine ndikufuna ndikufunse iwe chinachake.” Anati, “Kodi ndi ulaliki wuti umene ndinalalikira umene unakupangitsa iwe kumverera mwanjira imeneyo?” Iye anati, abusa, kapena anati, “Tsopano dikirani miniti,” anati, “ndi—ndi—ndi nyimbo iti ya kwayara?”

<sup>277</sup> Iye anati, “Oh, ine ndithudi ndimakonda kuyimba kumeneko uko ku tchalitchi, abusa.” Iye anati, “Ine ndimakonda uthenga uliwonse umene inu mumalalikira, chifukwa iwo umachokera mu Bukhu labwino ilo, ndipo ndimadziwa kuti ndi zoon. Koma,” anati, “sizinali zimenezo.” Anati, “Iye anangogogoda, ndipo ine ndinayang’ana pozungulira apa, ndi kuwona momwe Iye analiri wabwino kwa ine, chimene Iye anandipatsa ine.” Iye anati, “Lamlungu mmawa, Ine ndidzapita kutsogolo kumeneko kumene inu mwayima.” Iye anati, “Ndidzakupatsani inu dzanja langa lamanja,” anati, “chifukwa ine ndinapereka mtima wanga kwa Ambuye, kumusi komwe kuzungulira phiri uko.” Iye anati, “Ine adzabatizidwa, ndipo ndidzatenga malo anga pambali pa mkazi wanga. Ndipo ine ndikakhala pamenepo mpaka Ambuye atandiitana ine mmwamba.” Mwaona, iye anangopezeka kuti anayang’ana mozungulira ndipo anawona momwe Mulungu analiri wabwino kwa iye.

<sup>278</sup> Ndine wa mishonare. Ngati inu mungayang’ane kunja kupyolera mmaso amene ine ndikuyang’anamo tsopano, ndi kuwona malo Achimwenye, anthu anjala aang’ono amenewo, amayi akufa ndi njala pa msewu, ana awo aang’ono sangathenso kulira, chifukwa cha njala, ndipo tangoganzani zimene ife tinali nazo pano lero. Tayang’anani pa magalimoto amene mwabweramo. Tayang’anani pa zovala zimene mwavala. Tayang’anani momwe muliri olemera. Mzanga, kodi inu simukumverera kugogoda kwakung’ono uko penapake?

Tiyeni tipemphere.

<sup>279</sup> Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ndi mitima yathu, pamene maminiti tsopano akudutsa, pafupifupi maminiti seveni kuti

ufike masana. M'bale wanga, mlongo, sayansi imatiuza kuti ndi maminiti atatu kuti ifike pakati pausiku. Tsopano ngati inu mungakhoze kungoyang'ana mozungulira, ndi kungoganiza kwa miniti. Ana anu aang'ono akhala pamenepo pafupi ndi inu. Ndi osokonekera ubongo angati . . .

<sup>280</sup> Tamuyang'aneni mkazi wanu wabwino, m'bale, ndipo taganizani ndi amuna angati amene ali ndi madola mamillioni, ndipo amakonda mkazi ndi mtima wake wonse, iye ndi chidakhwa. Iye angapereke millioni yake yozizira kuti mkaziyo azimukonda momwe mkazi wako amakukondera iwe. Ndipo iwe, mkazi, ndi akazi angati . . .

<sup>281</sup> Ndi amayi angati pano mmawa uno ali ndi ana awo aang'ono, ndi abambo angati; bwanji, mai, pali amuna ambiri akuyang'ana pa kabedi, kanthu kakang'ono kopinimbira, mwana wamng'ono wosawuka, wolumala, ndipo taonani pa ana abwino amene inu muli nawo. Mukuona? Ndipo ambiri achikulire pang'ono, mwinamwake . . .

<sup>282</sup> O Mulungu! Pali zinthu zambiri, ngati mungayang'ane. Iye wakhala wabwino kwambiri kwa ife Achimerika. Tsopano inu simungamverere kuti mukufunika kukhala ndi mankhwala a mmaso pang'ono, mmawa uno, "Tsegulani maso anga mowonjezera pang'ono, Ambuye, tsegulani maso anga"? Monga mlongo wathu wokonedwa anayimba, "Diso Lake limakhala pa mpheta, mpheta yaing'ono chabe, ndipo ine ndikudziwa Iye amandiyang'anira ine."

<sup>283</sup> Tsopano Iye akuyang'anira pa inu tsopano. Kodi inu mungangomva, pansu penapake, kugogoda pang'ono monga *chonchi*, [M'bale Branham akugogoda pa chinachake—Mkonzi.], "Ine ndikuchezero, mmawa uno"? Ndi ulemu waukulu kwambiri umene ungaperekedwe, ngati mungakumverere kugogoda kumeneko pa mtima panu.

<sup>284</sup> Kodi mungangokweza dzanja lanu, ndikuti, "Ndi ichi, Ambuye, ndi chithandizo Chanu ndi chisomo Chanu, kuyambira lero, ndidzakhala pafupi ndi Inu monga momwe ndimadziwira kukhala ndi moyo. Ndizo zonse zimene ndikudziwa momwe ndingakufunsemi Inu"? Mulungu akudalitseni. Mulungu akudalitseni. "Ndi thandizo Lanu ndi chisomo, lero, kuyambira lero, sindidzaiwala ichi."

"Taonani, Ine ndaima pakhomo, ndipo ndikugogoda. Ngati munthu aliyense . . ."

<sup>285</sup> Tsopano, kumbukirani, kodi Iye ankagogoda kuti, ku barani? Ayi. Ku bara? Ayi. Iye akugogoda kuti? Ku tchalitchi!

<sup>286</sup> "Ngati munthu aliyense amva Liwu Langa, ndi kunditsegulira Ine, Ine ndidzalowa ndi kudya ndi iye, ndi iye ndi Ine."



287 Wokonedwa Mulungu, mawu osweka aang'ono awa, osakanizika, ochepa amene anenedwa mmawa uno, mwanjira ina mulole Mzimu Woyera uwatanthauzire iwo ku mitima ya anthu.

288 Tsopano apo panali ochuluka, Ambuye, mwinamwake mwa handirede awa pano panali anthu twente kapena sarte amene anakweza manja awo. Ine ndiribe njira yodziwira basi chimene iwo amasowa, Ambuye. Koma ine ndikudziwa kuti masana ndi maminiti pang'ono chabe, ndipo chomwechonso Kudza kwa Ambuye; komabe, chisanu ichi chisanasungunuke pansu, ife tikhoza kuitanidwa, ndipo iyi ikhoza kukhala nthawi imene ingasinthe tsogolo lonse ngati iwo ati atsale kuno kapena apita mmwamba.

289 Wokonedwa Mulungu, modzichepetsa ife tikumulandira Yesu, ife tikuvomereza Mawu Ake onse. Tidzazeni ife, Ambuye, tidzazeni ife ndi Mzimu Wanu Woyera, kuti moyo wathu mwaokha uthe kubala chipatsocho. Perekani izi, Ambuye.

290 Tikhululukireni ife zolakwa zathu zambiri. Oh, ndife odzaza ndi izo, Ambuye. Ndipo ife tiribe kanthu kamene tingathe kupereka, Ambuye, chifukwa, chirichonse chimene ife tiri nacho, Inu mwachipereka icho kwa ife. Monga Gabe ananenera, munkhani yaing'ono imene tangoyikamba, "Inu, Inu ndithudi mumatikonda ife, Ambuye, kapena Inu sibwenzi mutachita izi." Ndipo, kuganiza, anthu awa akhala pano kuyambira mlawirira mmawa uno, akhala pano kuyambira eyiti koloko, ndi maora foro amene akhala muno. Iwo amakukondani Inu, Ambuye. Iwo amakukondani Inu. Tsopano, Atate, kodi Inu mungatumize mankhwala a Mzimu Woyera, tsegulani maso athu. Mulole ife . . .

291 Awa amene ali muno mu mzinda, mulole iwo athamangire ku chitsitsimutso icho usikuuno, mulole pakakhale kutsanulira koteroko! Perekani izi, Ambuye. Mulole chitsitsimutso chachikale chiyambire kuno mu mzinda. Perekani izi. Mumudalitse munthu aliyense amene akupereka, mmodzi aliyense wa antchito Anu mdziko lonse, amene akupanga kuyesetsa. Mukhale nawo iwo, Ambuye, ndipo muwathandize iwo.

292 Mutsegule maso athu kuti tithe kuwona, mochuluka ndi mochuluka, mawonekedwe a Khristu. Perekani izi, Ambuye. Tikhululukireni machimo athu.

293 Ndipo tsopano awa amene anakweza manja awo, Atate, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu. Alandireni iwo. Tsopano ndibwereza Mawu Anu Omwe, Ambuye, amene, "Miyamba ndi dziko lapansi zidzalephera, koma," Inu munati, "Iye," chimene ndi mlowam'malo wa umwini, "Iye amene amva Mawu Anga . . ." Ambuye, iwo mwina anali osweka ndi ophweka, koma winawake anawamva iwo. Mbewu inagwa. "Iye amene amva Mawu Anga ndi," mlumikizi, "kukhulupirira pa Iye

amene anandituma Ine,” chifukwa Iye anachita ichi, “iye ali nawo (nthawi yomweyo) Moyo wosatha, ndipo sadzabwera kuchiweruzo mtsogolo, koma wadutsa kuchoka ku imfa kupita ku Moyo.” Iwo anakweza manja awo, Ambuye. Iwo anaswa (lirilonse) lamulo la sayansi; mphamvu yokokera pansi imakokera manja athu pansi. Koma iwo atsimikizira kuti mwa iwo muli mzimu, umene utha kumva kugogoda pa chitseko, ndi kufikira ndi dzanja lawo lamanja kupita Kumwamba. Tsopano tsegulani chitseko. Tsegulani, Ambuye, ndipo mulowemo. Ndife Anu. Tilandireni ife, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye  
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine  
Nandigulira chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

<sup>294</sup> Inu mukumukonda Iye? Ndikudabwa ngati ife tingatseke maso athu, mphindi yokha. Tsopano kuchokera mmitima yathu, ndi manja athu mmwamba.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye  
Chifukwa . . .

<sup>295</sup> Ife tikuvomereza kugogoda Kwanu, mmawa uno, Ambuye. Manja anga ali mmwamba. Manja athu onse ali mmwamba, Ambuye.

Ndipo . . .

Tsopano dzaloweni mkati, Ambuye Yesu. Bwerani mmitima yathu ndipo mudzadye ndi ife, ndipo ife tidzadya ndi Inu.

Mtengo wa Kalvare!

<sup>296</sup> Kodi inu mumamukonda Iye? Oh, ine ndikuganiza Iye ndi wodabwitsa kwambiri! Sichoncho inu? Kodi inu simukumverera Kukhalapo Kwake kukukhala ngati kukukwechani inu? Ine ndikumverera mwachipembedzo kwenikweni pakali pano, basi—ndikungomverera bwino kwenikweni, chinachake cha izo.

Chikhulupiriro changa chikuyang’ana kwa  
Inu,  
Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,  
Mpulumutsi Waumulungu;  
Tsopano ndimveni pamene ndikupemphera,  
Chotsani machimo anga onse,  
O ndiloleni ine kuyambira lero  
Ndikhale Wanu kwathunthu!

<sup>297</sup> Tsopano ine ndikufuna inu, pamene ife ting’ung’udza ndime yotsatira iyi ya nyimbo yokongola imeneyo, nyimbo yakale ya mpingo, Ine ndikufuna kuti mugwirane chanza ndi winawake. Mungokhala pampano wanu, mungonena, “Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ndine wokondwa kukhala nanu pano!” Tiyeni tichite zimenezo. [M’bale Branham akung’ung’udza, *Chikhulupiriro Changa*

*Chikuyang'ana Kwa Inu—Mkonzi*]. Mulungu akudalitseni inu, Carl, wokondwa kukhala pano . . . ? . . .

<sup>298</sup> Tangoganizani, manja a Methodistu anagwira a Pentekoste, a Baptistu anagwira a Presbateria.

O mulole . . . kuyambira lero  
Ndikhale Wanu kwathunthu!

<sup>299</sup> Tsopano pamene tikuyimba pang'onopang'ono tsopano, inunso, kuchokera pansu pa mtima wanu. Inu mukudziwa, utatha Uthenga wokwecha, wodzudzula, Ine ndikuganiza ndi zabwino kulowa mu Mzimu ndi kuyimba, kukoma kwa Mzimu Woyera.


<sup>300</sup> “Oh nzokoma bwanji kuti abale akhale pamodzi mu umodzi!” Baibulo linati, “Ziri ngati mafuta odzozera amene anali pa ndevu za Aroni, amene ankatsikira mpaka mphepete mwa chovala chake.” Ndinu anthu odabwitsa kuno. Ine ndikuyembekeza kubwereranso kuti ndidzakuwoneni inu kenanso Yesu asandziyitane ine, kapena Zakachikwi. Ngati ine sinditero, ine ndidzakuonani inu kutsidya kwa mtsinje uko. Ndidzakakumana nanu pa mtsinje. Ameni. Ndi mgwirizano.

Pamene njira ya moyo ya mdima ndiyenda,  
Ndipo chisoni chindizungulira ine,  
Inu mukhale Namulondola wanga;  
Ingitsani mdima ukhale usana, (Kuwala  
kwakung'ono Kuja kumene iwo  
amakukamba.)  
Mupukute mantha a chisoni achoke,  
O ndiloleni ine kuyambira lero  
Ndikhale Wanu kwathunthu!

<sup>301</sup> Khomo lililonse mulitsegule! Oh, mungokhudza kabatani kakang'onoko, ndipo muwawone iwo onse akupita mozungulira mkomberowo; akuti, “Lowani, Ambuye Yesu, mukhale Ambuye wanga, zonse zanga.”

O ndiroleni ine kuyambira lero, (ndisati,  
ndikuloleni Inu muyime pa chitseko,)  
Ndikhale Wanu kwathunthu!

<sup>302</sup> Inu amene munakweza manja anu ndipo mukufuna kuti mutsogoleredwe kuyandikira kwa Ambuye, Ine ndikukufunsani kuti mupite kumusi ku chitsitsimutso usikuuno. Ndipo ine ndikutsimikiza abusa kumeneko akutengerani inu kuchokera kuno kupita ku nyumba ya alendo. Iye ali ndi sikisi pensi, kapena chirichonse chimene chinaperekedwa, kuti asamalire, ndi vinyo ndi mafuta oti azikatsanuliramo. Iye akhoza kutsiriza ntchitoyo.

<sup>303</sup> Mulungu akudalitseni inu tsopano. Ine ndibwezera msonkhano kwa, ine ndikuganiza, M'bale Williams, kapena aliyense amene ali . . . 

65-0206 Zitseko Mu Chitseko  
Americana Hotel  
Flagstaff, Arizona U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)